


## *Mpingo Mdi Chikhalidwe Chake*

 Matenda osapezekapezeka a mwana woti akumbukiridwe makamaka mmawa uno mu pemphero, kotero ife zedi tikufuna konse kuti tichite izo. Madokotala sali kudziwa nkomwe. Iwo anawapatsa iwo dzina la mtundu winawake, koma ine ndikuganiza iwo anangolipanga lina kuti awapatse iwo, iwo—iwo sanali kudziwa chimene iwo anali. Ndipo, koma Khristu akudziwa chimene iwo ali. Ine ndikhoza kukuuzani inu chomwe iwo ali, ndi mdierekezi, ndiko kulondola, Mdierekezi. Dzina lanji limene iwo akufuna kumupatsa iye, bwanji, izo ziri kwa iwo. Koma ndicho chimene iye ali, iye iye ali, onani, mzimu woyipa. Tsopano tiyeni, tonse palimodzi, kamodzi limodzi tsopano, “*Kungokhulupira*,” aliyense abwere tsopano.

Kungokhulupira, kungokhulupira,  
Zonse ndi zotheka, kungokhulupira;  
Kungokhulupira, kungokhulupira,  
Zonse ndi zotheka.

<sup>2</sup> Ambuye akuchizani inu, mlongo. Tiyeni timupempherere msungwanayu tsopano pamene ife tikuweramitsa mitu yathu.

<sup>3</sup> Atate Athu Akumwamba, zikuwoneka ngati ine sindingakhoze basi kuzichotsa izo mu malingaliro anga. Msungwana wamng'onoyo apo, akufa, iye ndi wokonedwa wa winawake. Iye ali chirengedwe Chanu, ndipo Satana akumulanda iye moyo wake wawung'onowo. Ine ndikupemphera kuti mu Dzina la Khristu kuti Inu mubweze dzanja la imfa, mumuthamangitsire kumbuyo mdani ameneyo. Inu, Ambuye, Amene mungapange Nyanja Yofiira kuchita khoma pa mbali iliyonse, ndi kuwapatsa ana a Israeli, zomwe ziri Zanu, ulendo wotetezeka powoloka nyanja ndi kukalowa mu dziko lolonjzedwa. Mulungu, ife tikupemphera lero kuti Inu musunthire kumbuyo chotchinga chirichonse ndi kumulola mwanayo akhale moyo. Izo zapatsidwa kwa ife kuti tipemphe. Ndipo, ngati gulu la anthu lokhulupirira mwa Inu, ife tikupempha mu Dzina la Yesu kwa kuchiritsidwa kwa mwanayo. Amen.

<sup>4</sup> Lero ziri mwa mtima woyamikira kuti ine—ine ndabwera kwa inu kachiwiri mu Dzina la Ambuye Yesu. Ine ndinabwera kunyumba molawirira pang'ono chabe kuchokera ku Louisiana. Ndimaganiza kuti mwinamwake ngati ine nditafika kuno lisanafike Lamlungu ine ndikanadzakhala ndi Sande sukulu. Ndiyeno nyengo inali yotentha mowopsya kumeneko, mwakuti ife...uku kungakhale mwapakati, kuzizira mmawa uno kufanizitsa ndi Louisiana. Inu sibwezi mutakhala mu chipinda monga chonchi mopanda chokupizira, mu

Louisiana, pakadayenera kukhala choziziritsa kapena bwezi inu mukukomoka.

<sup>5</sup> Ndipo kotero ine ndabwera kotero kuti ndingokhala ndi kupuma kwa tsiku-kapena-awiri ndisanachoke tsopano pomwe pano, wa ku Northern Saskatchewan, sabata lotsatira, ndipo ndizo mpaka ku Prince Albert. Ndiko mpaka komwe misewu ikupita mu dziko, kuchokera ku mbali yina. Iwo umawoloka njira yonse kupita ku dziko lopanda nkomwe misewu ina iliyonse, ndipo kopanda kanthu koma Amwenye ndi Maeskimo kumbuyo mkati kudutsa kumene ife tikupita nthawi iyi. Kotero ife tiri ndi anthu ambiri omwe ati adzakhale pa msonkhano uwo ochokera konsekonse ku Canada. Ena a iwo adzabwera mpaka kuchokera ku Chigwa cha Kumadzulo, iwo akuti, akubwera uko. Ndipo ine ndithudi ndikukhumba mapemphero a inu anthu, kuti Mulungu akakomane nafe ife ndi kutipatsa ife msonkhano woposa, wochulukuka, wawukulu kwa ulemerero Wake. Izo zakhala kwa zaka zinai zina kapena zisanu chikhalireni ndiri mu Canada. Ndipo ine ndiri nawo amzanga ena olemekkezeka kwenikweni kumeneko, amene ali anthu abwino kwambiri.

<sup>6</sup> Ndipo kotero iwo ali okhulupirika kwambiri kupita ku tchalitchi. Ziribe kanthu kuti kwazizira motani, iwo amadzikulunga mu bulangeti ndi kukhala pa zikuku, ndi kumawongolera kavalo kwa mailosi makumi atatu, kuti akafike popita ku tchalitchi. Iwo amayenda kupyola kusuntha kwa chisanu ndi china chirichonse, ana ndi akulu. Iwo onse amasonkhana palimodzi. Ndipo banja limodzi limatenga lina ndipo iwo amayamba kuyenda, ndipo iwo amapita. Ndiyo—ndiyo nsembe imene iwo amapanga imene imawapangitsa iwo kuti apeze zochuluka chotero kuchokera mu msonkhano. Pamene palibe nsembe, palibe zochulukuka kwambiri kwa msonkhanowo. Iwe uyenera kufika pansu kwenikweni ndi kuchita chinachake chimene chimapweteka moyipa kwenikweni, uyenera kuyika kumbali zinthu zina ndi kusiya ntchito, ndi kuchita *izi* kapena *izo*, kuti ukafike popita ku tchalitchi ndi kukamuwonetsa Mulungu kuti iwe umamukonda Iye, ndipo iwe ukapanga nsembe kuti upite, ndi pamenepono pomwe iwe umapeza chinachake kuchokera kwa iwo.

<sup>7</sup> Izo ziri ngati ana anga. Billy Paul, ine ndinkaganiza ine ndikana...Ine sindinakhale nako kalikonse pamene ine ndinali mwana. Mayi anakonda kupeza mwinamwake thumba limodzi la switi ndipo iwo ankayeza izo, zidutswa ziwiri kapena zitatu kwa mmodzi aliyense. Mwinamwake za Khristimasi ife timalandira nyanga yaying'ono yachitini kapena basitole yaying'ono ya chipewa, kapena chinachake. Ndipo ine ndinkawawona ana ena ali ndi zikuku ndi njinga ndi zinthu, zovala zabwino ndi zikhoto zofunda. Ndipo ine—ine, izo zinkangondipanga ine kumverera moyipa kwambiri, ine ndinati, “Ngati ine ndikanati ndidzakhale ndi ana aliwonse

anga anga, ine ndidzawachitira iwo chirichonse chimene ine ndingakhoze.” Chabwino, ine ndikanakhala wololera kupita ndi njala kuti ndipeze chinachake cha ana anga. Ndipo pamene ine ndinakhala moyo... Pamene Billy anali chabe mnyamata wamng’ono, ine ndimamupezero iye njinga ya magudumu atatu, ndi kumupezero iye chirichonse. Ndipo Meda amayesa chirichonse, kuti apereke zovala zake zomwe ndi zinthu, kuti amupezero iye chinachake. Koma inu mukudziwa chiani ife tinayamba kupeza? Ine ndinamugulira iye njinga yaying’ono ya magudumu atatu, ndi uta wawung’ono ndi mpaliro, ndi chirichonse. Ine ndimampeza iye ali ndi—ndi supuni kapena ndodo, kunja mu bwalo, akukumba penapake. Mukuona? Ine ndinati, “Ena otsatirawo sadzakhala monga choncho.” Mukuona? Inu mungomupatsa aliyense chirichonse pa dzanja lawo kumene, iwo sachifuna icho. Ndi chinachake chimene iwe umayenera kuchitira nsembe!

<sup>8</sup> Ndipo umo ndi momwe chipulumutso chiriri. Ndi nsembe yamphumphu. Iyo ili, M’bale Roy. Ndiyo—ndi nsembe imene iye uyenera kuti uzichita tsiku lililonse, chinachake kuti—kuti uyandikire kwa Mulungu ndi kuchita chinachake. Ndipo ine ndikudziwa kuti ndi nsembe kwa inu nonse mmawa uno, kukhala mu chipinda chotentha ichi. Pamene ife takhala muno, tiyeni ife tiyike malingaliro athu pa Nsembe yayikulu imene mtundu waanthu unayamba wapatsidwapo kuti uyichite, imeneyo inali Yesu Khristu pamene Iye analamulidwa kuti abwere ku dziko lapansi kuti adzafe mmalo mwathu. Osati chokhacho ayi, koma moyo Wake unatsikira mpaka mu gehena ndipo unali kumeneko kwa masiku atatu ndi usiku, ndipo pa tsiku lachitatu Iye anawuka, ndipo tsopano anakwera mmwamba, akukhala pa dzanja lamanja la Mulungu, Kumwamba, akupangira mapembedzero pa kuvomereza kwathu kwa chitetezero Chake ndi chisomo Chake chimene chaperekedwa kwa ife.

<sup>9</sup> Tsopano uko mu...kumtunda uko kumene ife tikupita, uko kukakhala anthu ambiri, osawuka kwenikweni, osawuka kwenikweni, amachita kukagulitsa imodzi ya ng’ombe zawo, ziwiri kapena zitatu za nkhosa zawo, kapena chinachake, kuti afike pobwera ku msonkhano. Eskimo wachikulire amabweretsa mwinamwake zina za zikopa zake ndi kumazigulitsa izo, zimene iye amazisowa kwenikweni kwa banja lake, kuti abwere uko. Mmwenye wamalonda amayenera kuchita chimodzimodzi. Tsopano, ife tikhoza pang’ono pokha kuwapempherera anthu amenewo, sitingatero ife? Ndipo ife tikupemphera kuti Mulungu adzawapatse iwo chinthu chachikulu.

<sup>10</sup> Tsopano, ndi kotentha, ine sindikufuna kuti ndikusungeni inu motalika. Ndipo ine ndikufuna ife mmawa uno kuti tiyike malingaliro athu, basi ife tisanakhale ndi pemphero pa odwala, pa *Mpingo Ndi Chikhalidwe Chake*. Ndipo, tsopano, ine

ndikumverera kuti masiku pang’ono apitawo kuti Uthenga kwa mpingo unapatsidwa kwa ine ku Shreveport, Louisiana, ndipo ine—ine ndikukhulupirira ndizo zikhalidwe za mpingo. Ndipo ife tikuti tiyang’anane naye Mulungu ndi izo mmawa uno, ndi kupemphera ndi kumupempha Mulungu kuti atithandize ife. Sindikulinga kutenga mafikidwe omwewo, koma timupemphe Mulungu kuti atithandize ife mu tsiku ili limene ife tikukhalamo. Ndipo basi tisanati . . . Ili ndi Baibulo lopambana lakale, koma basi mmenemo mwagona zonse za Moyo Wamuyaya.

<sup>11</sup> Ndipo kumbukirani, Mawu ali Mulungu, Mulungu sali mochuluka kuposa Mawu Ake. Ndipo ife sitiri mochuluka kuposa mawu athu, ndipo ngati ife tipanga . . . Ndithudi, tsopano, inu ndi ine mu kuyima kosiyana . . . ganizo, limodzi ife tikhoza—ife tikhoza kunena kuti, “O, ine ndichita chinthu chinachake,” ife timatanthauza icho mu mtima mwathu, koma zochitika zikhoza kuwuka zimene ife sitingakhoze—ife sitingakhoze kuchita izo zimene ife tinanena kuti ife tikanachita. Koma Mulungu sangakhoze kuchita zimenezo, chifukwa Iye ndi wopandamalire ndipo Iye amadziwa chirichonse, ndipo chirichonse chimene chinakhalapo konse, chiti chidzakhalepo. Kotero, Iye sangakhoze kupanga neno pokha Iye akanadziwa kuti Iye akanaliyimira ilo kumbuyo.

<sup>12</sup> Ndipo Abrahamu, pamene iye anali usinkhu wa zaka zana, iye anazitcha zinthu izo zimene zinali palibe, ngati kuti izo zinali ziripo. Tsopano ine ndikunena izi ngati chilimbikitso kwa amene ati apemphereredwe, odwala. Abrahamu anazitcha zinthu zimene zinali palibe, ngati kuti zinali ziripo, kuwerengera kuti Iye Amene anapanga lonjezo anali wokhoza kuti alichite, kapena, kusunga icho chimene Iye anali atalonjeza. Tsopano, pamene Mulungu anamuza Abrahamu, pamene iye anali zisanu ndi chimodzi . . . makumi asanu ndi awiri ndi zisanu, ndipo Sarah anali makumi asanu ndi limodzi ndi zisanu, kuti iwo anali oti akhala ndi mwana, bwanji, izo zinali palimodzi zosatheka. Ndipo iye anakhulupirira zimenezo ndi kumuyembekezera mwanayo, ndi kumuwerengera mwanayo bwinobwino ngati kuti ali pamenepo, kwa zaka makumi awiri ndi zisanu mwanayo anasabwere konse. Ndipo Abrahamu anali zana pamene mwanayo anabadwa, ndipo Sarah anali makumi asanu ndi zinai, chifukwa iye anamukhulupirira Iye. Ndipo iye anazitcha zinthu zimene palibe, ngati kuti izo zinalipo.

<sup>13</sup> Tsopano, ndizo kwa odwala ndi osautsidwa oti apemphereredwe. Ziribe kanthu chimene mavuto anu ali, kaya muli . . . mtundu wanji wa matenda amene inu muli nawo, kaya inu muli moyipa kwambiri motani, pamene inu mumulandira Khristu, Mawu Ake, ndiye inu mumatcha zinthu zimene ziripo, ngati kuti izo panalibe, ngati izo ziri motsutsa kwa Mawu a Mulungu. Tsopano, Mulungu anati, “Pemphero la chikhulupiriro lidzapulumutsa wodwala.” Chabwino, ngati Mulungu ananena

izo, icho chikukhazikitsa izo. Ndiye tiyeni tiyike malingaliro athu, chiyembekezero, ndi kuchita ngati kuti izo zachitidwa kale. Izo zatsirizidwa kale pamene ife tizilandira izo.

<sup>14</sup> Chipulumutso chiri njira yomweyo. Ife timachikhulupirira icho, kuchilandira icho, kuchikhulupirira icho mu mitima yathu, kuyenda mpaka pamaso pa Mulungu ndi kumulandira Khristu ngati Mpulumutsi wathuwathu, ndi kumulandira Iye. Ngati inu muli pano mmawa uno, ndipo wochimwa, ndipo wosapulumsidwa, ndipo inu mukufuna kuti muchiritsidwe, inu mukudwala, choyamba funani Ambuye. Mulandireni Iye ngati Mpulumutsi wanu, ndiye matenda amenewo achita kuchoka kumene. Chirichonse chimene chiripo, ingoyikani lingaliro lanu lonse (ku chirichonse chimene inu muli nacho) pa Munthu yense, Khristu Yesu, chinthu chirichonse chikhala chiri chabwino.

<sup>15</sup> Kotero tsopano sungani malingaliro anu pa izo, chifukwa ine ndinanena mawu pang'ono awa chifukwa cha iwo amene ali odwala ndi osautsika, kotero kuti ine ndati ndiyankhule mmawa uno kwa mpingo ndi chikhalidwe. Pakuti ine ndikumverera kuti ngakhale machiritso Auzimu ali ododometsa, koma pamene ine ndinali mu Shreveport, ine ndinali kokha ndi pafupi misonkhano itatu ya machiritso pamene ine ndinali kumusi uko, itatu, kapena mwinamwake inai, mwa kupambana, kuchokera mu masiku khumi ndi limodzi. Ndi chofunikira kwambiri kulalikira kwa miyoyo ya anthu kuposa momwe izo ziliri kuyika nthawi yochulukira chotero pa machiritso Auzimu. Ngakhale, anthu amene akudwala ndi osowa, Mulungu akhoza kuwachiza iwo. Ndipo izo zakhala kale zitatsimikiziridwa kuzungulira dziko, kuti Iye amatero. Koma chinthu chachikulu, tsopano, ndi kwa moyo umene sudzafa konse. Thupi lidzafa. Koma moyo sudzafa konse, ndipo ife tiyenera kuusunga umenewo ndendende ndi molunjika naye Mulungu.

<sup>16</sup> Ine kawirikawiri ndanenapo izi. Ine ndikufuna chirichonse chichitidwe, pakuti pamene ine nditi ndidzafike pa mtsinje mmawa umenewo, ine sindikufuna vuto lililonse pamenepo. Ine ndikufuna kudzakhala ndi chiphatso changa mu dzanja langa, kuyembekezera dzina langa. Ndipo ine ndikufuna kunena, monga Paulo wakale, M<sup>b</sup>bale Creech, “Ine ndikumudziwa Iye mu mphamvu ya chiwukitsiro Chake.” Kutu pamene Iye andiyitana ine kuchokera pakati pa akufa, ine ndidzatuluka . . . Ine ndikufuna kumudziwa Iye mu mphamvu ya chiwukitsiro Chake.

<sup>17</sup> Kotero, tsopano, Iye Amene ali Mlembi wa Bukhuli, tiyeni tiweramitsire mitu yathu ndi mitima kwa Iye mphindi chabe.

<sup>18</sup> Ndipo, Mulungu, Atate athu, ife tikudza kwa Inu tsopano, kuti tipemphe kuti Inu mutsegulire Mawu Anu kwa ife. Ife tikhoza kukokera mmbuyo masamba, koma Mzimu Woyera

wokha ukhoza kutsegula Mawu. Kotero tsegulirani Iwo mmawa uno kwa ife, Atate, ndipo mutipatse ife zochulukuka mopitirira za chisomo Chanu. Ife tikuyembekezera pa Inu. Ndipo mulole Mzimu Woyera ulowe mu Mawu, ndi kuwapereka Iwo kunja kupyolera mu milomo ya munthu kwa mitima ya anthu, ndipo mulole Iye awatenge Iwo ndi kuwayika Iwo mu mtima uliwonse basi monga ife tiri nako kusowa. Ndipo pamene misonkhano ikhala itatha, ife tiri okonzeka kuti tibwerere ku nyumba zathu, ife modzichepetsa tidzaweramira mitu yathu ndi kukupatsani Inu kuthokoza ndi mayamiko, chifukwa cha zonse zimene ife taphunzira kwa Inu ndi chimene Inu mwatichitira ife. Mu Dzina la Khristu ife tikupempha izi. Amen.

<sup>19</sup> Kuwerenga kwa Mawu, uko mu Yohane Woyera, mutu woyamba, inu amene muli ndi Mabaibulo ndipo mukanafuna kuti muwerenge ndi ine kapena kulemba izo pansi kwa mutu. Ndipo ife tiwerenga mutuwo kuchokera mu Mawu, ndiyeno tiyeni tipemphere, ndi kuti Mzimu Woyera udzatenge nkhani kuchokera mu Mawu kuti uwupereke kwa ife. Ife tikhoza kuwerenga Iwo, ife amene tiri okhoza kuti tiwerenge tikhoza kuuwerenga Iwo, koma Mulungu yekha angakhoze kuyitulutsamo nkhaniyo. Mutu ukhoza kuwerengedwa, chifukwa Iwo ndiwo Mawu Ake, komano—nkhaniyo iyenera kuperekedwa ndi Mulungu. Tsopano, mu Yohane Woyera, mutu woyamba, ndipo tiyeni tiyambire pa ndime ya 28 ndi kuwerenga mmusi mpaka ku ya 32, malimodzi.

*Zinthu izi zinachitika...kutsidya kwa Yordani, kumene Yohane anali kubatiza.*

*...tsiku lotsatira Yohane pomuwona Yesu akubwera kwa iye, ndipo anati, Taonani Mwanawankhosa wa Mulungu, amene achotsa machimo a dziko.*

*Ndipo uyu ndi iye amene ine ndinati, Pambuyo pa ine pakudza mwamuna amene ali wokondedwa ine ndisanakhalepo: pakuti iye analipo ine ndisanakhalepo.*

*Ndipo ine sindimamudziwe iye ayi: koma iye... koma kuti iye ayenera kuti...awonetseredwe kwa Israeli, chotero ine ndabwera kumabatiza ndi madzi.*

*...Yohane anachitira umboni, kuti, Ine ndinawona Mzimu ukutsika kuchokera kumwamba ngati nkunda, ndipo iwo unadzakhala pa iye.*

Ine ndikufuna kuti ndiwerenge izo kachiwiri, ndime yotsiriza iyo, ndime ya 32.

*Ndipo Yohane anachitira umboni, kuti, Ine ndinawona Mzimu ukutsika kuchokera kumwamba ngati nkunda, ndipo iwo unadzakhala pa iye.*

<sup>20</sup> Tsopano alole Ambuye kuwonjezera madalitso Awo ku Mawu. Ine ndikufuna inu kuti muyesere ku—kuti mugwire mawu

aliwonse ngati ife tingathe. Kodi inu mukukhoza kundimva ine bwino bwino kutali kumbuyoko? Chabwino, kodi inu mukukhoza kundimva ine kumbuyo uko? Ngati inu mukukhoza, inu kwezani mmwamba dzanja lanu. Ndizo zabwino.

<sup>21</sup> Tsopano, ine ndikufuna kuti ndiyankhule kwa inu mmawa uno pa—pa fanizo, mwa njira ina moti ngakhale—munthu yemwe sali wampingo kwambiri mkati muno angakhale wokhoza kuti amvetse. Tsopano, ife timabwera ku tchalitchi kudzadzikonza tokha. Ife timabwera kuti tidzadzipange tokha anthu abwinoko, Akhristu abwinoko, mbadwa zabwinoko, abambo abwinoko, mayi abwinoko, oyandikana nawo abwinoko. Ife timabwera chifukwa Khristu watuza ife kuti ngati ife titati tibwere, kupempha chirichonse mu Dzina Lake, pamene ife tiri titasonkhana palimodzi ochuluka monga awiri kapena atatu, Iye akanakhala ndi ife ndipo akanapereka izo kwa ife. Chotero, chingakhoze kukhala chiyani choposanso, kukhala chabwino konse kwa ife lero kuposa kudziwa kuti ife tiri pa mpingo kuti tidzadzipange ife ni kukhala abwinoko, kuti tikulitse kumvetsa kwathu? Ndi angati amene akanati anene kuti, “Ndicho chimene ine ndadzera pano”? Tiyeni tiwone, “Ine—ine ndikufuna kumvetsa kwabwinoko.” Ndipo ife sitingakhoze—ife sitingakhoze kukhala nako kumvetsa kwabwinoko kupatula izo . . . Ndipo ngati ife titi tikhale nako kumvetsa kwa Mulungu, iko kuyenera kubwera kuchokera mu Mawu a Mulungu, pakuti Mawu ali chimene Mulungu anatipatsa ife kuti tidyetse miyoyo yathu yanjala. Ndipo Mzimu Woyera unatumizidwa kuti utenge Mawu a Mulungu ndi kuti utidyetse ife ndi Mawu. Inu mukuziona izo? Onani, ife . . . Mzimu Woyera watumizidwa kuchokera kwa Mulungu, kuti utenge Mawu a Mulungu ndi kuti uwapereke Iwo kwa ife monga ife tiri nako kusowa. Tsopano, ine ndiri wokondwa kwambiri kuti Mulungu anapanga kupereka konga kumeneko. Sichoncho inu? Kuti Iye akanamatidyetse ife.

<sup>22</sup> Ife ndife nkhusa za ubusa Wake. Ife tiyankhula pa izo pang’ono pokha, nkhusa. Ndipo ife ndife chinthu chofutukukapatatu cha Mulungu, ndipo pamene Iye angakhoze kukhala nawo ulamuliro wamphumphu wa ife Iye akhoza kutitsogolera ife ndi kutilondolera ife.

<sup>23</sup> Tsopano, icho chinamukomera kwambiri Mulungu, kuti pamene Iye anatumizira Yesu ku dziko lapansi, kuti icho chinamukomera Iye kuti amuyimire Iye ngati chinyama, ndipo chinyama chimenecho chinali mwanawankhosa. Kale kutali mu chiyambi, mu Munda wa Edeni, mu mithunzi yotsogolera ya kudza kwa Yesu, Mulungu anapereka nsembe kapena anali ndi mwanawankhosa kuti akhale chopereka cholowammalo mu mithunzi yotsogolera ya kudza kwa Khristu. Tsopano, ine ndadabwa kawirikawiri chifukwa chiyani kuti Mulungu akanamuyerekezera Khristu ngati chinyama, ngati chamoyo. Koma ife tinafika podzapeza kuti Mwanawankhosa, chifukwa

chimene Iye anasankhira mwanawankhosa, mwanawankhosa ndi chamoyo chofasitsitsa ndi chaulemu kwambiri mwa zolengedwa zonse zimene ziripo pa dziko lapansi. Palibe kanthu kenanso kofatsa ndi kaulemu kuposa mwanamwankhosa wamng'ono, wosalakwa chotero, osati wodzikwaniritsa-yekha. Iye—iye sali wamwano. Iye ndi chofatsa, cholengedwa chaching'ono chonyozeka. Ndipo pamene Mulungu ankati akamuyimire Khristu kwa dziko, Iye anamuyimira Iye mu mwanawankhosa.

<sup>24</sup> Tsopano, koma pamene Mulungu, Atate Mulungu, Yehova, anali kuti akadziyimire Yekha kuchokera Kumwamba, Iye anayimiridwa mwa yofatsa kwambiri, yodzichepetsa kwambiri ya mbalame zonse zimene zimawuluka mmwamba, imene ili, nkhooda. Palibe mbalame yaulemuko kuposa nkhooda. Ine ndinapanga phunziro ndithu pa moyo wa mbalame ndi pa zinyama, ndipo nkhooda ndi mbalame yosamvetseka kuchokera ku mbalame ina iliyonse imene imawuluka mmiyamba. Nkhooda ndi ya—ya—yachikondi. Nkhooda ndi yofatsa. Ndipo nkhooda ilibe ndulu, ndi yokhayo mu banja la mbalame imene ilibe ndulu. Ndicho chifukwa inu simungayiwone nkhooda kulikonse koma ikuzungulira pamene pali njere ndi mbewu. Tsopano, m. . .

<sup>25</sup> Mu chombo, umo munali nkhooda. Ndipo nkhooda ikuyimiridwa mu malo ambiri mu Baibulo. Ndi chiphiphiritso cha Mzimu Woyera. Ndiponso mwanawankhosa akuyimiridwa mu malo ambiri a Baibulo, ngati Khristu, mu Chivumbulutso, njira yonse kubwerera ku Genesis, ndipo chomwechonso ili nkhooda.

<sup>26</sup> Ndipo mu Bukhu la Genesis, nkhooda inali mu chombo, ikukhala pa chisa ndi—ndi mbalame zina zonse za mu mlengalenga; ndipo imodzi ya iyo inali khungubwe, khwangwala. Ndipo khwangwala ndi imodzi ya mbalame yadyera imene ilipo, khwangwala ndi katawa, ine ndikuganiza, ndi pafupi mbalame zadyera zimene ife tingakhoze kuzipeza. Khwangwala ndi mbalame ya moyo wautali kwambiri, ndipo iyo imakhala moyo (iwo amanenedwa) kwa, nthawizina, zaka mazana awiri kapena atatu, zimene khwangwala. . . Chingolopiyo amakhala moyo wautali kuposa pamenepo.

<sup>27</sup> Koma nkhooda ndi chinyama chimodzi kapena mbalame imodzi imene simakhala nayo ndulu. Tsopano, khwangwala akhoza kukhala pamwamba apa ndi kumadya pa nyama yakufa. Inu simudzayiwona konse nkhooda pozungulira nyama yakufa imeneyo. Iyo singakhoze kupirira izo. Fungo la iyo mu mphuno zake, iyo siingakhoze kupirira nalo. Ilo likanamupangitsa iye kudwala. Izo sizingakhoze basi kupirira chirichonse chimene chikuwonongeka, chikuvunda. Izo sizingakhoze kupirira izo, kotero iyo siyingakhoze kuzidya izo. Ngati iyo ikanati idye izo, izo mwamsanga zikanaipha nkhooda, chifukwa chimene



chimagaya chakudya ndi kusefukira kwa ndulu kulowa mmimba imene imagaya chakudya. Ndipo ngati mulibe ndulu yoti ipite mkati ikapange izi, ndiye icho chikanaipha nkhundayo. Kotero inu nthawizonse mudzayipeza nkhunda ikuzungulira pamene pali chinachake chaukhondo, chinachake chimene chiri champhumphu.

<sup>28</sup> Tsopano, khwangwala ndi wosiyana. Tsopano, ingozindikirani khwangwala pokhala choyimira cha wachinyengo. Khwangwala akhoza kukhala apo pa—pa nyama yakufa ndi kudya mochuluka basi monga iye akufunira kutero, ndi kuwulukira pomwepo kumunda ndi kukadya tirigu, ukonso. Koma nkhunda siyingakhoze kudya tirigu ndiyeno nkuwulukira pa nyama yakufa.

<sup>29</sup> Kotero, wachinyengo, munthu akhoza kukhala wachinyengo ndipo nkumadya zonse zinthu zauzimu, ndipo zinthu zabwino ndi zinthu zoyipa. Koma Mkristu wobadwa-kachiwiri weniweni sangakhoze kulekerera zinthu zimene ziri zolakwika, ndipo angadye kokha kuchokera ku chinthu chabwino. Zindikirani zimenezo! Pamene inu mumuwona munthu amene angakhoze kupita ku zovina, kupita kunja ndi kukamwa, kupita kunja ndi kukakhala mu tchimo, kubwerera ku mpingo ndipo mwinamwake kumafuula mochuluka basi monga woyera, ndi chiyani icho? Iye ndi mkangaziwisi, iye akhoza kudya zonse chinthu chovunda ndi chinthu chabwino. Koma Mkristu weniweni sangakhoze kulekerera zinthu zimenezo mwakuwonjezera kulikonse, pakuti iye wadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo. Ndipo mwamsanga izo zikanamutsutsa iye chotero, malingaliro omwe a izo, mpaka izo zikanamutsutsa iye mpaka iye akanakhoza kutembenuza nkhope yake ndi kuyenda chochokapo. O, ndi chithunzi chotani!

<sup>30</sup> Tsopano, mwanawankhosa ndi kanthu kakang'ono kofatsa kwambiri. Iye samatha, iye sangakhoze kudzithandiza yekha. Iye sali wodzidalira-yekha, chifukwa iye sangakhoze kudzithandiza yekha. Kuno nthawi ina kale ine ndinali kupita ndikudutsa mu msipu pamene ine ndinali ndikulondera, ndipo ine ndinapeza nkhoza yaying'ono, ndipo zonse za izo zinani zitachoka kwa iye mwanjiraina, ndipo iyo inali yonse itakulunguzidwa mu mulu pang'ono wa waya waminga. Ndipo kanthu kakang'ono kosawuka kanali katagona pamenepo, kakuwukha ndi kulira. Ndipo ine ndinabwera pafupi ndipo ine ndinawona kutali kumtunda, pafupi theka la mailo, kunali khamu lonse la nkhoza. Tsopano, iye akanakhoza kugona pamenepo ndipo akhwangwala akanakhala akukolowola mu maso ake posakhalitsa ndithu ngati ife tikanapanda kumuchotsapo iye. Koma ine ndinakakamasula kanthu kakang'onoko, ndinamunyamula iye mu mkono wanga. Iye sanakane konse. Iye anagona mwakachetechete ndithu. Ine ndinamunyamula iye mu mikono yanga. Yoyamba—nthawi

yoyamba, mwinamwake, imene munthu anayikapo konse manja ake pa iye, koma iye anali wofatsa. Iye anali kulolera kuti akhale akutsogoleredwa. Iye anali kulolera kuti athandizidwe. Ine ndikuyembekeza inu mukuziona izo. Iye anali kulolera osati kuti ayesere kuti akane kapena kuti akankhe Chambuyo, kapena kuti alume. Anaankhosa samakankhira kumbuyo, iwo samaluma; iwo amangodzichepetsa okha. Ndipo kanthu kakang'ono aka, ine ndinamunyamula iye ndi kumukhazika iye pansi pa nkhusa zonse. Mu maminiti ochepa mayi wake anamupeza iye, momwe iye analiri okondwa! Tsopano, momwe ziriri zofanana izo ndi Mwanawankhosa wa Mulungu!

<sup>31</sup> Inu mukudziwa, kumene iwo amapita kukapha nkhusa, inu mukudziwa chimene chimatsogolera nkhusa ku nyumba yokapherako, ndi mbuzi. Koma mbuzi imalola kutsogolera nkhusa mpaka pa makako a ku nyumbayopherako, ndipo, ndiye basi nthawi imene iyo ifikitsa nkhusa pobwera mpaka pa makako, ndiye iyo imalumpha kuchokapo. Koma, o, iwo amati, pamene iwo akupita kuti akaphe mbuzi, ndiye iyo imakankha mwa voko. Mwaona?

<sup>32</sup> Ndipo umu ndi momwe Mdierekezi angati achitire. Iye ayesa kuwatsogolera ana a Mulungu mpaka mwankhaza kwambiri, koma pamene ifika nthawi yakuti iye afe, iye amakankha kwenikweni mwavoko ndiye. Umumu ndi momwe Mdierekezi amachitira izo. Ndipo umu ndi momwe nthawizina, msungwana wina wamng'ono wamawonekedwe-okhumbirika kapena mnyamta wina wamng'ono waushasha, ali ndi paketi ya ndudu kapena botolo la kachasu, akanati amutsogolere msungwana wamng'ono kumbali, mwanawankhosa, ali ndi wumutsatira wa winawake, kumpolozera ku zolakwika. "O, ziri bwino. Palibepo zakanthu kwa zonse izo zinthu zabwino-zabwino za mpingo." Koma mulole imfa imukanthe mnyamata wachikulire uyo nthawi imodzi, inu mumumve iye akulira, akufuula konsekonse pa dzikolo. Ndipo umu ndi momwe Mdierekezi amachitira izo.

<sup>33</sup> Koma mwanawankhosa ndi wofatsa kwambiri, mwakuti iye akhoza kutsogoleredwa. Ndipo ndicho chifukwa chimene Mulungu anamuyimira Khristu ngati Mwanawankhosa, ndipo Iyemwini ngati Nkhunda. Ndipo pa tsiku limene Yohane anamubatiza Yesu pa mtsinje wa Yordani, chimodzi cha zochitika zazikulu kwambiri zimene zinayamba zachitikapo, chinachitika apo pomwe. Zindikirani kukongola kwake! Mwanawankhosa, wofasitsitsa wa zolengedwa zonse za pa dziko lapansi, ndi Nkhunda, yofasitsitsa ya mbalame zonse za Kumwamba. Tsopano, ndiyo njira yokhayo imene iwo akanati adzakhale konse olumikizana. Ndi njira yokhayo imene Nkhunda ikanati konse ibwere pa Mwanawankhosa. Tsopano, pamene Nkhunda inabwera pansi, Yohane anamuwona Yesu, ndipo iye anati, "Taonani Mwanawankhosa wa Mulungu,

amene achotsa machimo a mdziko.” Ndipo Yohane anati, “Ine ndikuchitira umboni, ndauwona Mzimu wa Mulungu ngati Nkhunda ukubwera pansu, ndi kukhazikika pa Iye.” Aleluya! Pamenepo inu muli. Nkhunda ndi Mwanawankhosa zitalumikizana limodzi. Ndi pamene Mulungu ndi Munthu anakhala mmodzi. Ndipo pamene Kumwamba ndi dziko lapansi zinakumbatirana wina ndi mzake. Aleluya! Ndipo pamene Mulungu anapangidwa thupi, analibweretsa ilo, ndipo pamene Mulungu anabwera pansu kuchokera mu mawonekedwe a Mzimu ndipo anapangidwa kukhala Munthu ndipo anakhala pakati pathu. Ndipo pamene Umuyaya wonse unakumbatirana wina ndi umzake. Ndi pamene mtundu wakugwa wa anthu a Adamu ndi Yehova Mulungu ndi mngelo aliyense anabwera palimodzi, pamene Mulungu ndi munthu anapangidwa mmodzi, pa tsiku lalikulu lachikumbutso lija pamene Yohane anamubatiza Yesu.

Tsopano, bwanji ngati uyo akanakhala nkhandwe? Kuyimba kokoma kwa Nkhunda sikukanakhala kokhoza kuti kuyime pafupi ndi nkhandwe.

<sup>34</sup> Ndi chiyandinso chiri chokongolerapo kuposa madzulo mochedwa kuzimva nkhunda zimenezo zitakhala panja apo ndi kuyimba mwakanthawi? Nditangoti ine ndataya mkazi wanga ndi mwana... Ine sindikanamulola wina aliyense kuti adziwe chimene ine ndinali kuchita. Ine ndinkakonda kulowa mu galimoto yanga yakale, ine ndinkayendetsa kunja kuwoloka msewu kuno, kupita kunja apa ku manda a ku Walnut Ridge, kukakhala pamtunda pamenepo pa mbali ya mtengo ndi kumayang’ana mmusi ku manda. Ine sindimakhoza basi kuwaleka iwo. Zinkawoneka ngati ine sindikanakhoza kupilira izo mopitiriranso. Ine ndikuganiza, mwana wanga wamng’ono, akugona kumeneko, wausinkhu miyezi isanu ndi itatu. Momwe iye anakondera kugwira manja ake aang’ono ndipo anakhoza kundifikira ine, ndipo ine ndikayimba lipenga kapena kunena chinachake kwa iye, ndipo iye ankati “guu-guu,” akufikira ndi manja ake aang’onowo. Ndipo ine ndinkakhala pansu pambali ya mtengo, makamaka pamene iwo amafika madzulo. Ndipo kumeneko kunkakonda kukhala nkhunda yakaleyo imene inkakhala kunja kumeneko mu tchire, iyo inkayamba kuyimba. O, mai! Ine ndinayamba ndadabwapo ngati iyo inali moyo wachisavundi wa mwana wanga ukubwerera mmbuyo kuti udzayese kuti uyankhule kwa ine. Palibe chokoma kuposa kuyimba uko kwa nkhunda. Momwe iyo iliri yokonda! Iyo imabweretsa uthenga. Momwe iyo imayesera kupangitsa mtendere! Kudzuka molawirira mmawa, kupita kunja mu ziyangoyango uko pafupi ndi kumene ine ndimakhala, ndi chinthu chamtendere bwanji icho chiri kuti umvetsere! Zitakhala pamwamba pa mtengo wawukulu wautali uwo, nkhunda zimenezo zikuyimba kwa ina ndi imzake.

<sup>35</sup> Tsiku lina, kumusi kwa M'bale Cox, manthu wakale wa nk'hunda anali ndi ana aang'ono awiri. Ndipo iwo anakhala pamwamba pomwe pa nyumba, kotero amphaka sakanakhoza kuwagwira iwo. Ndipo mayi wokalamba wa nk'hunda amakhoza kumawadyetsa iwo. Ndiye iye amabwera pansi ndi kuwatenga iwo ndi kuwapangitsa iwo kuti akwere mmwamba mu mtengo, ndipo iwo amakhoza kukhala pamenepo ali ndi makosi awo pozungulizana wina ndi mzake, ndi kumayimba ndi kupanga chikondi, utali wa tsiku lonse, tinkhunda tiwiri tating'ono, timabunda taulemu.

<sup>36</sup> Ndipo ine ndinaganiza za momwe Mulungu, (nk'hunda ndi mbalame yokonda chotero) ndipo Nk'hunda, Mulungu, pofuna kupanga chikondi ndi zinthu Zake zaumunthu. Mulungu amafuna kuti azikonedwa. Mulungu akufuna kuti azikukondani inu. "Mulungu analikonda dziko chotero, Iye anapereka Mwana Wake wobalidwa yekhayo, kuti aliyense amene akhulupirira mwa Iye asati adzawonongeke, koma kuti akhale nawo Moyo wosatha." Odalitsidwa akhale Ambuye! Ndiye Mulungu, pofuna kuti apace chikondi, Iye amayenera ku china . . . kupanga chinachake chokondeka. Iye amayenera kupanga chinachake chaulemu monga Iyemwini. Iye amayenera kupanga chinachake chimene chikanakhoza kukonedwa. Iye amayenera kupanga chinachake cha Chikhalidwe Chake Chomwe.

<sup>37</sup> Iwe sukanakhoza kukonda kanthu kamene sikanali ka chikhalidwe chako chomwe. Kukonda kuyenera kulumikizana nacho chikondi. Mwamuna ndi mkazi wake ayenera kukondana wina ndi mzake, ngati iwo akanati apace konse muyezo. Banja liyenera kukondana wina ndi mzake, ngati iwo angapange konse muyezo. Chinachake choti chizikonedwa! Iwe umafufuza kulikonse, umupeze msungwana woti akhale mkazi wako amene iwe umamukonda. Iye amafufuza, kuti apeze mwamuna amene iye angakhoze kumukonda.

<sup>38</sup> Mulungu amafufuza, kuyesa kuti apeze moyo umene Iye angakhoze kuwukonda. Kotero, Iye anadziyimira Yekha kuno pa dziko lapansi ngati Nk'hunda yaulemu ndi Mwanawankhosa waulemu. Ngati Mwanawankhosa ameneyo akanati pa miniti imodzi itenge konse chikhalidwe cha nk'handwe yaukali, Nk'hunda ija ikanayamba kuwuluka Kwake mwamsanga, iyo ikanapita kutali.

<sup>39</sup> Koma m—m—mwanawankhosa, iye alibe malingaliro alionse aakulu a iyoyokha. Mwanawankhosa ndi chinthu chimodzi, pamene iyo yasochera, iyo imasochera mopanda chiyembekezo. Nkhosa siingakhoze kupeza njira yake yobwererera. Ndicho chifukwa mbuzi imayitsogolera iyo ku imfa yake. Iyo siyingakhoze kupeza njira yake, nk'hosa imene yasochera. Ndicho chifukwa Mulungu anatifanizitsa ife kwa nk'hosa. Pamene ife tatayika, ife tatayika. Palibe njira yomwe ife

tingakhoze kudziyeza mwatokha. Ndipo pali njira imodzi yokha kuti ichtire izo, ndiyo, kudzipereka tokha kwa M’busa wa khamulo, ndipo Iye amachita kutsogolera.

<sup>40</sup> Tsopano, monga ine ndikuzindikira Mwanawankhosa uyu ndi nkhusa palimodzi. . . Mwanawankhosa ndi Nkhunda, kani, palimodzi, iwo anapanga chimodzi. Ndiye penyani momwe Nkhunda inatsogolera Mwanawankhosa, Mwana wa Mulungu. Momwe Iye analiri waulemu, akudziwa kuti Iye anali kupita kokaphedwa. Momwe Iye analiri waulemu, nthawizonse osayesa kuti achite Mwayekha, osayesa kuti akhale wokwana-mwayekha. Iye anati, “Ine sindimachita kanthu mpaka Atate atandisonyeza ine poyamba, ndipo Atate amakhala mwa Ine.”

<sup>41</sup> Tsopano, chinthu china chimene mwanawankhosa ali, mwanawankhosa ndi wololera kuti apereke maufulu ake. Tsopano, Mulungu akufuna ife kuti tikhale anaankhosa, koma pali nthawi zochulukira kwambiri zimene ife sitimafuna kuti tipereke maufulu athu, kupinyolitsa maufulu athu. Ambiri a inu mumati, “Chabwino, ine ndiri nawo maufulu, M’bale Branham.” Ndizo zooni, koma kodi iwe uli wololera kuti upinyolitse maufulu ako? Kodi ndiwe wololera kupereka maufulu ako, kuti Mulungu akhoze kukutsogolera iwe? Ndilo lomwe liri vuto ndi mipingo yathu lero, mu chiwengero chachikulu, kuti ulemu wa Mwanawankhosa wa Mulungu. . . Ife timayenera kuti tikhale anaankhosa, ife takhala china chirichonse osati anaankhosa. Ndicho chifukwa, mwamsanga pamene ife titenga kachitidwe kameneko, Nkhunda ya Mzimu Woyera imayamba kuwuluka Kwake ndi kuchokapo.

<sup>42</sup> Ngati Mwanawankhosa wa Mulungu akanati apange ukali woyamba ngati nkhandwe, kapena akanati achite chirichonse chosiyana kwa chimene Nkhunda yaulemu ikanachilolera icho, Nkhunda ikanayamba kuwuluka Kwake. Iyo ikanachokapo mu miniti.

<sup>43</sup> Ndipo ndicho chifukwa lero kuti ife tikudabwa, “Chavuta ndi chiyani ndi mpingo wa Chipentekoste?” Ndi chifukwa chakuti ife tatengera pa chikhalidwe chosiyana. Ife tatengera pa chikhalidwe chimene, “Ife tikufuna maufulu athu. Ife tichita zimene ife tikuzidziwa kuti ndizo zolondola kuti uzichite.” Ndipo ife timakhala amwano. Ife timakhala awukali. Ife timakhala osayanjanitsika. Ife timalola kupsya mtima kubwera mkati. Ife timalola umbombo kubwera mkati.

<sup>44</sup> Mwanawankhosa, pamene iyo ifika nthawi. . . Iye amakhala nawo ubweya wake wake, ndiwo maufulu ake. Iye amakhala nawo ubweya wake, koma iwo amamutenga mwanawankhosa ndi kumuponyera iye pa zipika, ndi kumangirira miyendo yake pansu. Iye samakankha, iye samakangana. Inu mumangotenga maufulu ake kuwachotsa kumene kwa iye, chifukwa iye ndi mwanawankhosa. Iye sangakhoze kuchita kanthu kena

kalikonse, chifukwa ndicho chikhalidwe chake. Koma nthawi ina ingodutsanipo njira ya Mkhristu, inu mudzapeza ngati iye ali mwanawankhosa kapena mbuzi. Inu mudzapeza chimene iye ali, mupingeni apo iye nthawi imodzi. Ndipo ndicho chifukwa lero kuti mipingo yathu ili mu chikhalidwe chimene iyo ili.

<sup>45</sup> Ife tadzitcha tokha mwanawankhosa wa Mulungu. Akazi ndi mwamuna, palimodzi, ayamba kuchita chirichonse osati ngati anaankhosa a Mulungu. Inu muyang'ane pa iwo akupita pansu mu msewu, ali ndi kabudula, tsitsi lodula, zopoteka zonse mu tsitsi lawo. Ndipo zaka pang'ono zapitazo, inu mumatcha. . . inu, iwo. . . inu simukanakhoza kuwalemba ganyu iwo kuti achite zimenezo. Ndiyeno iwe umadabwa chifukwa chimene chimene mpingo uliri mu chikhalidwe chimene iwo ulimo. Ndi chifukwa chakuti inu mwatenga chikhalidwe cha nkhandwe kapena mbuzi, mmalo mosunga kufatsa kwaulemu. Ndipo inu mumati, "Ndi mwayi wanga, M'bale Branham." Ine ndikudziwa kuti ndi mwayi wanu. "Ometa amadula tsitsi. Ndipo malingana ngati ometa ati azidula tsitsi, kodi ine ndiribe ufulu?" Ndiko kulondola, ndiwo mwayi wanu wa Chimereka. Koma kodi ndinu lolera kuti muwupereke iwo kunjira, kuti mukhale mwanawankhosa? Kodi ndinu wololera kuti mudzipereke nokha?

<sup>46</sup> Ndipo akazi inu, osati kale litali, inu mumapita ku msewu. . . Ndi zopusa kuti uyang'ane momwe akazi akuvalira lero. Ndipo ine sindikuyankhula za Apresbateria ndi Amethodisti, ine ndikuyankhula za inu akazi a chiyero. Ukapita pansu mu msewu, ndipo ziri. . .

<sup>47</sup> Ine ndinali nawo mtanda wawung'ono wopachikika patsogolo pa galimoto yanga, ndipo winawake anati kwa ine, anati, "Billy, kodi iwe ukudziwa ndicho choyimira Katolika?"

<sup>48</sup> Ine ndinati, "Ndi liti pamene Akatolika anapeza gawo pa mtanda?" Palibe! Icho sichiri choyimira cha chikhulupiro cha Chikatolika; ndicho choyimira cha chikhulupiro cha Chikhristu. Chikhulupiro cha Chikatolika ndi woyera wamng'ono wakufa, Maria kapena—kapena munthu wina wakufa amene iwo amamupembedza. Ife sitimapembedza anthu akufa. Ife sitimapembedza Cicilia Woyera ndi oyeri onse osiyana awo. Ndicho Chikatolika, chimene chiri mawonekedwe apamwamba a zamizimu. Koma mtanda umayimira Iye Amene anafa ndipo anawuka kachiwiri.

<sup>49</sup> Ndipo ine ndinati, "Ine ndimausunga uwo pamenepo, poyang'ana pa msewu. Zaka makumi awiri ndi zisanu zapitazo, kapena makumi atatu, pamene ine ndinali pafupifupi wakhungu, ine ndinamulonjeza Mulungu kuti ngati Iye akanati achize maso anga ine ndikanamayang'ana pa chinthu choyenera." Ndipo ine ndinati, "Kulikonse kumene iwe uyang'ana, ndi opandaumulungu chotero, akazi ovala mwatheka, ndi amaliseche atagona mu mabwalo ndi paliponse.

Ine ndimayang'ana pa mtanda mmalo mwakuyang'ana, ndi kukumbukira chimene Khristu anandichitira ine, ndi kupotoloza mutu wanga kwa chinthucho...chimene chiri cha Mdierekezi." Aleluya!

<sup>50</sup> Ndipo uko, anthu, musati munene kuti ndi "Chipresbateria, Chikatolika," ndi Chipentekoste! Ameni. Inu mukuti, "Ine ndiri nawo ufulu wotero, M'bale Branham." Ndiko kulondola, koma ngati inu mukanakhala mwanawankhosa, inu mukanapinyolitsa maufulu anu. Ndipo pamene inu mupita mukuchita monga choncho, Mzimu Woyera, Nkhunda yaulemu, imayamba kuwuluka Kwake pomwepo. Iyo siingachititsidwe manyazi ndi inu. Ayi, ayi, ayi. Inu musamaganize kuti mupita mukuchita monga choncho ndi kuwusunga Mzimu Woyera. Inu simungakhoze kuchita izo! Baibulo linanena chomwecho. Inu muyenera kupinyolitsa anu...Chabwino, kunena, "Akazi onse akuchita zimenezo."

<sup>51</sup> Ndipo inu amuna, inu zinthu zosawuka, zopanda mafupa, zachikazi, inu, amene mungawalole akazi anu kumachita chinthu chotero ngati icho, izo zikusonyeza chomwe inu mwapangidwa nacho. Ndicho chifukwa inu mulibe Mzimu Woyera monga inu mumanenera kuti muli nawo, kapena inu mukanakhala ndi chokwanira Chinachake pa inu kuti chimupangitse iye kuchita ngati dona kwa kutalika komwe iye akhale ndi inu, mulimonse. Ameni. Izo zikumveka mwa kudula, kwa kachitidwe-kachikale. Koma ndicho chimene mpingo ukusowa lero, ndiko kuchapa kwa kachitidwe-kachikale, kwa Mzimu Woyera, ndi kupachikidwa ndi kuwumitsidwa, ndi kusitidwa, nawo Mzimu Woyera. Zedi!

<sup>52</sup> Ndi chikhalidwe chotani dziko lalowamo! Momwe iwo amapita kunja pa msewu ndi kumapitiriza! Momwe inu mumakanikizira mutu wanu mu televizioni Lachitatu usiku, ndi kusapita ku tchalitchi! Momwe kuti inu...Bwanji, koma, palibe mwana mu dziko...amadziwa zonse za yemwe David Crockett ali. Ndipo bodza lakuda ilo, kumanena kuti iye anapha chimbalangondo pa usinkhu wa zaka zitatu, inu mukudziwa kuti ilo ndi bodza, koma inu mumawalola ana anu kupangitsa mutu wawo udzaze ndi zimenezo. Ndipo palibe gawo limodzi mwa chimodzi pa zana amene anadziwa konse kanthu kalikonse za Yesu Khristu. Ndi chifukwa chakuti dziko ili layipitsidwa kwambiri! Fuko ili, lopusa chotero ndi kutali chotero kwa Mulungu, lawukana Mzimu Woyera.

<sup>53</sup> O, inu mukuti, "Ine ndimapita ku mpingo ndipo ndimafuula." Inu mukhoza kumachita zimenezo. Koma, mpaka Mwanawankhosa waulemu wa Mulungu uja akhazikike mu mtima wanu, ndipo akupangitseni inu kuyetsa moyo wanu ndi kumachita ngati munthu wosiyana, izo sizikuchitirani inu ubwino uliwonse kuti muzisamdziwa Chikhristu. Inu muyenera kukhala nacho icho. Ameni.

<sup>54</sup> Ine ndinapita kukalowa mu nyumba kuno osati kale litali, kukachezera munthu wodwala, ndipo dona anali atagona, atakhala pamenepo. Ndipo Oswald wamng'ono uyo anabwera mkatimo, chipewa chitakhala pa mbali ya mutu wake, anati, "Mayi, kodi chakudya chamadzulo chakonzedwa?"

<sup>55</sup> Iye anati, "Wokonededwa, ife sitinakhale nayo nthawi" anati "mmawawu kuti tipeze chakudya chirichonse." Anati, "Ine ndikukukonzera iwe sangweji," anati, "apo pali malalanje ena."

<sup>56</sup> Iye anayenda kupita apo ndipo analitenga lalanjelo, anayang'ana pa ilo, analuma pa ilo, analiponyera ilo momenyetisa khoma mwamphamvu monga iye akanathera, madzi ache anayenderera pansi, anati, "Ngati ndizo zonse zimene inu muli nazo pa malo ano, ndiye ine ndipita kunja," monga choncho.

<sup>57</sup> Ine ndinaganiza, "O Mulungu, iye akadayenera kukhala wanga kwa pafupi maminiti asanu!" Mnyamata, ine ndikanakungunula chikopa kuchichotsa pa iye mwakuti iye sakanadziwa kuti icho chinali chitakungunulidwa kuchichotsapo! Koma iwo atakhala pamenepo, kumchitira chisoni ndi kumusasatitsa. Chimene iye akusowa ndi kachitidwe-kachikale ka kusenda kwa miyendo. Ndicho chimene ife tikusowa, manyumba ena a kachitidwe-kachikale kachiwiri, ndi alaliki ena amene ati ayime kuseri kwa guwa ndi kulalikira Choonadi, ndi kuchiyala Ichu apo pamene Ichu chikuyenera kukhala pamenepo. Amen. Ndizo zoon. O, mai!

<sup>58</sup> Maria wamng'ono anapondetsa phazi lake laling'ono, ndi kulozetsa mphuno yaying'ono iyo mmwamba ndi kuitembenuza milomo iyo yaying'ono kwambiri yolochedwa zofiira (zopangidwa ndi Max Factor) mmwamba mu mlengalenga, ndi kuyang'anitsa mutu wake wawung'ono mmwamba ndi kuchoka mnyumbamo. Ndi chamanyazi bwanji! Ana akukhala osamvera bwanji! Baibulo linati iwo adzakhala. Lemba linati iwo adzakhala. Momwe iwo ati adzakhali, momwe iwo ati adzachitire, ndi zinthu zimene zikuchitika mu dziko lero, ndi chifukwa chakuti iwo akwiyitsira kutali Mzimu Woyera.

<sup>59</sup> Zaka zingapo zapitazo. Ine ndikupita kumusi tsopano mu masiku angapo kukakondwerera kugwa koyamba kwa Mzimu Woyera mu Amereka, zaka makumi asanu zapitazo chaka chino, ku msonkhano wakale wa ku Azusa Street, msonkhano wa chipentekoste mu Los Angeles, kumene iwo anali nako kugwa kwawo koyamba kwa Mzimu Woyera, pamene anthu anasonkhana pamodzi. Pamene Khristu anabwera pansi pakati pa anthu amenewo, iwo anali basi aulemu, basi amtendere. Iwo ankakhala miyoyo yaumulungu. Iwo ankakhala miyoyo yodzipereka. Iwo anali lolera kugonjera. Iwo anali lolera kuti atsoqoleredwe ndi Mzimu Woyera. Iwo sankasamala chimene anthu ankanena, iwo anali "akachitidwe-kachikale," kaya iwo



amati iwo anali “openga” kapena chiani za izo, iwo anali lolera kuti atsogoleredwe ndi Mzimu Woyera.

<sup>60</sup> Koma, lero, o, mai, ndi zopakira paudala ndi bokosi la zopakapaka, ndipo atavala akabudula, ndi kutulukira pa msewu, bwanji, ndicho chamanyazi! Ndipo kumadzitcha okha, “ali ndi Mzimu Woyera.” O, inu mukuti, “Koma ine ndinayankhula mu malirime.” Inde, ndipo Mdierekezi amatero, nayenso. “O, ine ndinafuula.” Ndipo Mdierekezi amatero, nayenso. Mdierekezi akhoza kutsamzira chirichonse chimene Mulungu ali nacho, kupatula chikondi, ndipo iye sangakhoze kutsamzira chikondi. Eya.

<sup>61</sup> Ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa, pamene inu munayamba kuchita zinthu zimenezo, inu munalekerera pa zigwiriro, inu munayamba kunyengerera, ndiye mpingo unayamba kutenga makuluku pang’ono, timalingaliro pakati pawo, ndipo uyu anati, “Inu mukudziwa, abusa basi ali *zakuti-ndi-zakuti* basi,” kapena “adikoni ali *zakuti-ndi-zakuti*.” Ndipo, chinthu choyamba inu mukudziwa, inu munamvetsera kwa izo! Ndipo ndicho chifukwa inu muli nalo vuto lochuluka chotero, ndi chifukwa chakuti inu mwayamba kumvetsera kwa Mdierekezi, ndipo mwatenga ukali mmalo momvetsera kwa Nkhunda yaulemu, Mzimu Woyera, Nkhunda ya Mulungu imene iti idzakutsogolereni inu ndi kukulondolerani inu, kukukondani inu ndi kukudalitsani inu.

<sup>62</sup> Nthawi yoyamba imene inu munatenga zazing’ono za nthawi ya kukwiya izo, Nkhunda imawulukira kutali nthawi yomweyo. Ndiko kulondola. Iyo siyingakhoze kupirira izo. Khalidwe lake ndi losiyana. O, Iyo siyingakhoze kupirira izo nkomwe. Ndipo inu mukayamba kuyankhula za oyandikana nawo anu, Iyo siyingakhoze kuyima nazo izo, Iyo siyingakhoze basi kupirira nazo izo. Iyo imangotenga kuwuluka Kwake ndi kupita kutali kwambiri. Iyo siyingakhoze basi kupirira nazo izo mwa kutalika kwinanso. Nkhunda ndi yaulemu. Nkhunda ndi yofatsa, ndipo Nkhunda, ndipo—ndipo siyingakhoze basi kupirira chirichonse kokha ngati chiri mtundu womwewo wa khalidwe.

<sup>63</sup> Tsopano, Mulungu akhoza kukupangani inu khalidwe losiyana, mwamuna kapena mkazi, Iye akhoza kukupatsani inu khalidwe losiyana. Ndipo inu mukuti, “Chabwino, M’bale Branham, ife tingakhoze kuchita chiyani za izo?” Basi ingokhala mwanawankhosa kachiwiri. Ndi nyama ziwiri chabe zimene ziti zidzayanjane limodzi, ndizo nkhunda ndi mwanawankhosa. Nkhunda siyingabwere kwa china chirichonse koma mwanawankhosa. Ndipo ngati inu mwakhala mbuzi, ndiye chotsanipo mzimu wa mbuzi wakale uwo pa inu. Ndiko kulondola. Ngati inu mwakhala chinachake, chichotsenipo icho pa inu, ngati inu mwayamba kukhala wamanong’onong’o.

<sup>64</sup> Kuno nthawi ina, ine ndinalalikira molimba basi monga ine ndikanathera kulalikira mu mzinda winawake, ndipo uko kunali zikwi za anthu kumeneko. Ine ndinapanga kuyitanira paguwa. Ine ndinkaganiza ndinakuta dera lonse la tchimo, ine ndinakuta chirichonse chimene ine ndikanakhoza kuchiganizira. Usiku umenewo utatha msonkhano, mkazi wamng'ono wodula anayendera pafupi, iye anati, “Chabwino, M'bale Branham, ine ndikutsimikiza ndiri woyamikira kuti inu simunandikhudze ine usikuuno.”

Ine ndinaganiza, “Uyo ayenera kukhala Mkristu weniweni.”

Anati, “Inu simunandikhudze ine usikuuno.”

<sup>65</sup> Ine ndinati, “Chabwino, ine ndiri woyamikira kwambiri kumva zimenezo, dona, inu muyenera kukhala muli pafupi ndi Ufumu wa Mulungu.” Ndipo iye ananyang'amira kutali.

<sup>66</sup> Dona winawake atayima pamene. Ine ndinati, “Tanenani, kodi inu mukumudziwa mkazi ameneyo?”

“Inde.”

Ine ndinati, “Iye ayenera kukhala Mkristu weniweni.”

<sup>67</sup> Anati, “Chinthu chimodzi chimene inu munalephera kuchigunda usikuuno, M'bale Branham, chimenecho chinali miseche. Iye ndi mkulu wa amiseche mu dzikoli.” Pamenepo inu muli, ndi zimenezo, mwaona.

<sup>68</sup> Koma pamene inu mufika ku chimodzi cha zinthu zimenezo, ziribe kanthu kaya mlaliki wachigunda icho mu guwa kapena ayi, pamene inu muwona zinthu zachithupi izo za dziko, malingana ngati inu mulekererana nazo izo, inu muli kutali ndi Mulungu, ndipo Mzimu Woyera udzakhala kutali. Ndicho chifukwa misonkhano siiri momwe iyo inali kukhalira. Ndicho chifukwa kanjira ka utuchi sikanabadwe mmawa uno mu kachisi. Ndicho chifukwa misonkhano yayikulu ya msasa siiri kozungulira dzikoli, ndi chifukwa chakuti ife takwiyitsira kutali Nkhunda yaulemu ya Mulungu. Ndiko kulondola. Iye sangakhale ndi ife malingana ngati ife tiri osayanjanitsika, malingana ngati ife tikuchita miseche, “Ife tikufuna njira yathu!”

<sup>69</sup> Tsopano, ine ndikufuna inu kuti muzindikire, Mwanawankhosa anali Mwanawankhosa wachete. Baibulo linati, “Iye sanatsegule ayi kamwa Yake. Monga nkhusa pamaso pa oyisenga, Iye anali wosayankhula.” Iye sanatsegule kamwa Yake. Iye sanali munthu amene akufuna ufulu wake. Ayi, bwana, Iye anali wololera kulanditsa maufulu Ake. Iye anali Mwanawankhosa wachete.

<sup>70</sup> Koma, lero, o, mai, momwe ife tikufunira kusiyana kwathu! O, mai! “Ine ndikukuuzani inu, inu mungomulora winawake anene chinachake kwa ine, ine ndipita komweko kukamupeza

ieye, mnyamata, ine ndikamukhadzula iye. Ine ndikamuza wachinyengo wokalamba uja pamene ine nditi ndimuwone iye! Inu mungodikira mpaka ine nditamuwona iye! Adalitsike Mulungu, aleluya! Nhu-nhu!” Nkhunda imangotenga kuwuluka Kwake ndi kumapitirira kutali. Ndiko kulondola. Mzimu Woyera suli ndi inu kenanso, malingana ngati inu mukumverera mwa njira imeneyo. Ingolembani izo umo mu bukhu lanu, Iwo sudzachita konse izo. Mzimu Woyera sungakhoze basi kukhala pozungulira pamene mtundu wa mzimu uwo uli. Iwo uyenera kukhala mzimu wa mwanawankhosa, mzimu waulemu, kapena basi Iwo sungakhale ndi izo, ndizo zonse zimene ziripo kwa izo; ngati iwo suli waulemu, wofatsa, wotsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Ndipo ngati chirichonse chibwera apo, Iwo basi sumachizindikira konse icho, umangopitirira. Mwaona? Ndipo miniti yomweyo imene iwo utembenukira kumbali, inu mukudziwa, ndiyo kumene...pamene inu munatembenukira kumbali.

<sup>71</sup> Inu mukudziwa, tchimo loyamba limene linayamba la munthu nkutembenukira kumbali kwa miniti yokha. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Baibulo linanena choncho. Eva anatembenukira kumbali mphindi yokha, kuti amvetsere chimene Satana anali kuti anene, ndipo iye anajambula chithunzi chokongola kwambiri kwa iye mpaka iye anaganiza kwenikweni kuti izo zinali Choonadi. Ndipo iye anamvetsera kwa iye.

<sup>72</sup> Ndipo chinthu chokha chimene Mdierekezi akufuna kuti inu muchite, ndi kungotembenukira kumbali kwa maminiti pang’ono chabe. Iye akhoza kujambula chithunzicho, kunena, “Tsopano, yang’anani apa. Inu mukudziwa, m’bale, inu mukudziwa, mlongo, ngati iwo akanakhala anthu a mtundu wolondola, iwo sakanachita *izi*. Ngati iwo anangochita *izi* pomwe apa, inu mukudziwa.” Iye akhoza kupanga izo zenizeni kwambiri kwa inu mpaka icho chimakhala choonadi chenicheni. Kulondola! Koma kumbukirani, ndi Mdierekezi!

<sup>73</sup> Ine sindikusamala kaya iwo ali otsikitsitsa-pansi motani, motalikira bwanji momwe iwo adzinyazitsira mu tchimo, ndi ntchito yanu kuyika mkono mozungulira iwo ndi kuwanyamulira iwo mmwamba mwa chikondi cha Mulungu. Inu munali kuti pamene Nkhunda ya Mulungu anakunyamulani inu kuchokera mu thope la dongo? Ndi ntchito yanu, bwenzi wanga. Dziko ili likufa kusowa chikondi chapang’ono pokha. A...

<sup>74</sup> Ine ndikufuna inu muyizindikire nyama iyi, apanso, nyama yaying’ono iyi, iyo inali mwanawankhosa wachete chifukwa iyo siinati...pamene Iye analatiridwa, Iye sanalalate ayi aponso. Iye sananyoze ndi kumapitiriza, ndi kumakangana ndi kuchita ukali ndi kumapitiriza, Iye sanachite izo ayi. Pamene

winawake. . . Pamene Iye analalatrindwa, Iye sanalalate ayi aponso. Iye sanatsegule ayi kamwa Yake.

<sup>75</sup> Koma inu mungolola winawake achite chinachake kwa inu kapena ine, o, mai, ife timafufuma ngati chule akudya ngumbi, kufufuma ngati—ngati tsekwe wokalamba. “Ine ndikuwuzani inu pakali pano, iye kuponda pa zala zanga monga choncho kachiwiri, ine sindibwerera konse ku mpingo wakale uwo kachiwiri. Ayi, bwana! Adalitsike Mulungu! Aleluya! Anazereni akandilandira ine, a Pilgrim Holiness, iwo akanditenga ine. Aleluya. Ine sindisowa kuchita izo kenanso ayi.” Chabwino, Nkhunda imayamba kuwuluka Kwake.

<sup>76</sup> “Inu mukudziwa chiyani? Ngati wachinyengo wokalamba uja azipita ku mpingo umenewo, ine sindidzapitako konse kachiwiri. Adalitsike Mulungu, ine sindidzachita konse izo!” Pamene chinthu icho chikugundani inu, nkhandwe yakale yaukali ija, Nkhunda imatenga kuwuluka Kwake. Kulondola. Ndiye Mzimu Woyera wapita.

<sup>77</sup> Ndiye iwe umadabwa chavuta nchiani ndi iwe. Iwe umadabwa chavuta nchiani ndi iwe. Chifukwa chiyani iwe ulibe chigonjetso chonga chimene iwe unali kukhala nacho? Iwe wasintha khalidwe lako. Iwe wakhala mbuzi mmalo mwa mwanawankhosa. Iwe wakhala chinachake pambali pa mwanawankhosa.

<sup>78</sup> Inu uyenera kutenga Mzimu wofatsa kwenikweni uwo, “Mulole Mzimu Woyera unditsogolere ine kulikonse. Mulungu, ine ndikonde wochimwa aliyense, ziribe kanthu kumene iwo ali.” Malo a mtundu umenewo akalowa mu mtima wa munthu, ndiye inu muwona chinachake chikuchitika, moyo wanu.

<sup>79</sup> Inu mukuti, “Chabwino, M’bale Branham, kodi kulipo kukonza kulikonse kwa izo?” Inde, ingokhalani mwanawankhosa, ndizo zonse. Inu mukuti, “Chabwino, M’bale Branham!”

<sup>80</sup> Ine ndinakomana naye dona wamng’ono usiku wina, uko mu Shreveport. Billy ndi ine tinapita kumalo kuti tikapeze sangweji utatha kale msonkhano. Mkazi wamng’ono wokongola anabwera mmenemo, mwinamwake msungwana wamng’ono, kapena mwinamwake makumi awiri kapena chinachake monga choncho, wovala bwino. Iye anakhala pansi. Ine ndinazindikira iye ankangoyang’ana cha ku njira imeneyo. Ine ndinkangopitiriza kumadya. Maminiti angapo donayo atabwera mkati. Iye anati, “Muli bwanji?” Ndinayankhula kwa iye. Ndipo ine ndikumudziwa donayo anali Mlango Davis kumusi uko. Ndipo iye ndi dona wina wochokera ku Life Tabernacle, ine ndinkawadziwa iwo bwino, iye anabwera pamenepo ndipo anayankhula kwa ine, anapitiriza. Ndiye dona wamng’ono amene anakhala moyang’anizana, iye anati, “M’bale Branham, ujawu unali Uthenga wabwino usikuuno.”

<sup>81</sup> Ine ndinati, “Inu muli bwanji, mlongo?” Ine ndinati, “Zikomo inu, mochuluka kwambiri.” Ndipo ine ndinati, “Kodi ndinu membala wa Life Tabernacle?”

<sup>82</sup> Iye anati, “Ndiri.” Iye anati, “Inu mukudziwa, M’bale Branham, ine ndikanakhoza kuyimba mu kwayara, koma iwo akuchita zolepheretsa kumene kuja.” Iye anati, “Ine ndinali, o, zaka zambiri za kuphunzira kayimbidwe, ndi chirichonse.” Anati, “Ine ndimayimba masolo ndipo ndimayimba zinthu zina.” Anati, “Koma, ine—ine sindikanakhoza kuyimba, chifukwa iwo ali ndi—iwo ali ndi zolepheretsa kuti ‘palibe mkazi wodzipaka utoto angakhoze kuyimba—kuyimba mu kwayara.’”

Ine ndinati, “Chabwino, Mulungu alemekezeke chifukwa cha Life Tabernacle!”

<sup>83</sup> Iye anati, “Chabwino, ine ndikuuzeni inu, M’bale Branham,” iye anati, “Ine ndine Mkhristu.”

<sup>84</sup> Ine ndinati, “Ndiye, mlongo, pitani kunyumba ndi kukasukusula nkhope yanu, kapena chirichonse chimene inu mumachita.” Ine ndinati, “Kodi inu mukutanthauza kuti mudiwuze ine kuti inu mungalole kanthu kakang’ono choteroko ngati kuvala pang’ono za zinthu zakale izo pa nkhope yanu. . . .”

<sup>85</sup> Ndipo ine ndikhoza kutsimikizira kwa inu kuti izo zimabwera kuchokera kwa Mdierekezi. Ine ndikhoza kutsimizira kwa inu kuti palibe mu. . . Chiyambi cha izo chinali achikunja. Ndipo monse pamene inu muvala izo, ndi chilemba cha chikunja. Tsopano, ine ndangobwera kumene kuchokera ku Afrika, ndipo ine ndakhala mu nkhalango za Akafula ndipo ndazipeza chimodzimidzi basi kumene ndolo, kumene zinthu zonse izo zinachokera, ndi zonse izi, ngale zochuluka zitakulungidwa kuzungulira makosi anu ndi makutu ndi chirichonse, kumene izo zimachokera. Ndi achikunja. Ndipo Baibulo silikufuna Mkhristu kuti akhale wachikunja. Ndipo inu simukufuna. . . Ine sindikunena kuti inu ndinu wachikunja chifukwa chakuti inu mumachita izo, koma inu mukudzipanga nokha kuwoneka ngati mmodzi. Ndi chifukwa chakuti abusa anu sanati akuwuzeni inu Choonadi. Baibulo linanena choncho.

<sup>86</sup> Ndipo tsopano inu mukuti, “M’bale Branham, ine ndikuganiza ngati ine ndikhala ndi tsitsi lalifupi, ilo limandipanga ine kumva bwino ndi chirichonse chotero.” Ndiko kulondola, koma ngati inu mukanakhala ndi tsitsi lalitali inu mukanamva bwino. Ilo likanachotsa izo zonse pa khosi lanu, ndi kulikulunga ilo ndi kulipanga ilo mwabwino.

<sup>87</sup> Bwanji, kodi inu mukudziwa chimene Baibulo linanena? Kutu, mwamuna ali nawo ufulu womusiya mkazi wake ndi kulandira chisudzulo kuchokera kwa iye ngati iye adula tsitsi lake. Ngati iye adula tsitsi lake, izo zikusonyeza kuti iye akukhala mosawona kwa iye. Baibulo linanena choncho, I

Akorinto 12, fufuzani ngati Izo siziri zolondola. Iye amene. . . Mkazi amene adula tsitsi lake amanyozetsa mutu wake, amene ali mwamuna wake. Ndipo ngati iye ali wonyozetsa, iye ayenera kusudzulidwa ndi kuchotsedwa. Ndiko kulondola. Koma, onani, abusa samakuuzani inu konse zinthu zimenezo. Ndipo ndicho chifukwa chimene inu mumachitira momwe inu mukuchitira. Ndipo—ndipo mwamuna, Baibulo linati. . .

<sup>88</sup> Kuno osati kale litali kunali winawake amene analemba kuno ndipo anati, “M’bale Branham, ma—mabulauzi awa amene akazi amavala,” anati, “bwanji, ziri mwakuti m. . . inu simungakhoze basi kuwapeza konse mabulauzi panonso, ndipo izo zikanakhala zabwino kuti ife akazi Achikhristu tizivala zoterera izi, nayiloni, kapena chirichonse chimene chiripo chonga izo?”

<sup>89</sup> Ine ndinati, “Penyani, mlongo, pali chinthu chimodzi cha izo. Apa pali chinthu chimodzi choona. Inu mukhoza kuchita ichi: ngati inu simungakhoze kugula imodzi, iwo amagulitsa makina osokera, inu mukhoza kupanga imodzi.” Ine ndinati, “Ndiko kulondola, kuipanga iyo kuti izingowoneka. . .” Ine ndikukhulupirira. . . Inu mukudziwa, chimene chiri mu mtima mwanu ndi chimene chimadzifotokoza chokha. Momwe inu mumachitira ndi momwe inu mumapangira, izo zimasonyeza chimene chiri mwa inu.

<sup>90</sup> Ndicho chifukwa kuti zonse izi pano zoyipidwa ndi kukangana ndi kuchitanamiseche, ndi—ndi kubwezera miseche, ndi kumapitirizabe pozungulira mpingo, ndizo zimene zimaphwasula mpingo. Izo zimasonyeza kuti Mdierekezi analowa mkati mwa inu, ndipo izo zikusonyeza kuti Mzimu Woyera unakuchokerani inu. Tsopano, ine ndikudziwa kuti izo zikungowotcha phula kulikuchotsa mwa ena a inu, koma izo ziyenera kuchita izo. Izo ziyenera kuteru! Ndicho chimene izo zikunenedwera; osati kuti mukhale anzeru, osati kuti muzichita mokongola; koma kukuuzani inu pamene pali vutolo, chifukwa tsiku lina ine ndiyenera kuti ndidzayime ndi kupereka yankho chifukwa cha inu. Ndipo chifukwa kumene momwe inu mumachitira ndi momwe inu mumapangira, izo zimangosonyeza chimene inu muli. Ngati inu mwangokhala nako kupsya mtima kwakale kumene kudzawuluke kuchokera pa chigwiriro chake ndi zazing’ono chabe, ndi kufika kuno ndi kumapitiriza, kapena kutsutsa, kapena zoyipa ndi zinthu ngati zimenezo, izo zimasonyeza kumene izo zikuchokera.

<sup>91</sup> Tsopano pali chinthu chimodzi chokha choti muchite, chichotseni chinthu icho uko mmenemo, ndipo Nkhunda idzabwerera ku mtima wanu. Pamene nkhunda inapita kuchokera mu chombo, iyo inatulutsidwa kunjja. Koma iyo inabwerera ndipo inagogoda pa chitseko cha mdima mpaka Nowa anayilola iyo kulowa mkati. Mzimu Woyera uli pano. Mzimu Woyera ukufuna kuti ubwere mkati. Ndicho chifukwa

lero, kuti Mzimu Woyera, Iwo sunachoke kwa inu kwa nthawizonse. Iwo wangokhala kunja uko pa nthambi za mitengo penapake, kukonzekera kuti idz iwulutse Yokha chobwerera ndi kubwera kulowa mwa inu, ndi kukupatsani inu chikondi ndi mtendere ndi chimwemwe monga inu munkakhalira nazo. Zedi, Iwo uli. Iwo uli wokonzeka kuti uchite zimenezo. Iwo ukufuna kuti uchite izo. Iwo ukukhumba kuti uchite izo. Koma inu simukuwulola Iwo kuti uchite izo!

<sup>92</sup> Tsopano, ine sindikuyankhula kwa inu alendo. Ine sindikudziwa chimene abusa anu... Ine ndikuyankhula kwa Branham Tabernacle. Ine sindikuyankhula kwa inu anthu ochokera ku mpingo ina. Ine ndikuyankhula kwa Branham Tabernacle. Ndilo vuto kuzungulira pano.

<sup>93</sup> Ndicho chimene chimapangitsa Nkhunda kutenga kuwuluka Kwake. Mungomulola winawake ayambe kenakake kakang'ono pozungulira mpingo, ndipo chinthu choyamba, "O, kodi izo ziri choncho? O, anatero? Inu simukutanthawuza choncho?" Pomwepo kumene Mzimu Woyera umapita, kuwulukira kutali. Iwo sungakhoze basi kupirira mzimu wa mtundu umenewo. Malingana ngati chikhalidwe cha mwanawankhosa chija chikuchokerani inu, ndiye Mzimu Woyera wachokapo. Ndiko kulondola. Ndipo ndilo liri vuto lero. Ndicho chifukwa anthu ali mu chikhalidwe chimene iwo alimo, ndi chifukwa iwo amalola mzimu wolakwika kubwera mu mtima mwawo, mu moyo wawo. Tsopano ndicho chifukwa ife tiri . . .

<sup>94</sup> Baibulo linati ndicho chifukwa pali odwala ambiri ndi osautsika pakati pathu, ndi chifukwa cha zinthu zoterozo. Ife tiyenera kukhala aulemu. Ife tiyenera kukhala amtendere. Ife tiyenera kukhala mwanawankhosa, kotero kuti Nkhunda ikhoza kukhala ndi ife.

<sup>95</sup> Tsopano, kumbukirani, Nkhunda idzabwera. Inu munati, "O, M'bale Branham, musati mudiwuze ine kuti sindinalandirepo Mzimu Woyera. Aleluya! Uko, usiku kumeneko usiku wina, o, pamene Iye anabwera mkati, ine ndimakhoza kumangoyenda..." Zedi bwanji, ameneyo anali Iye! "O, ine ndinamverera bwino kwambiri, ine ndinamverera ngati ine ndikhoza kugwira mbalame iliyonse kuchokera mu mtengo ndi kuyikumbatira iyo ndi kuyikonda iyo. Munthu woyipisitsa amene anayamba wachitapo kalikonse kwa ine, ine ndinamverera ngati ine ndikhoza kuyika mkono wanga mozungulira iwo ndi kuwakumbatira iwo. O, M'bale Branham, momwe ine ndinamverera!" Zedi, umenewo unali Mzimu Woyera.

<sup>96</sup> Koma, inu mukuona, chifukwa chimene Iwo sukanakhoza kukhala nanu. Inu munali mwanawankhosa panthawiyo; koma pamene inu munadzakhala nkhandwe, Iwo umayenera kutenga kuwuluka Kwake. Palibe cholakwika ndi—ndi—ndi Nkhunda;

ndi inuyo, ndipo m. . . inu munalola mzimu umenewo kubwera kwa inu. “Kodi ine ndinawulola iwo, M’bale Branham?” Inde, pamene inu munapita kukamvetsera ku miseche ija, pamene inu munamvetsera ku bodza lija, pamene inu munapita kukanena, “Chabwino, ine ndiri nawo ufulu wotero!”

<sup>97</sup> Inu mulibe maufulu ayi! Inu munagulidwa ndi mtengo, umenewo unali mtengo wa Magazi ofunika a Mwana wa Mulungu. Inu mulibe maufulu ovomerezeka. Aleluya! Maufulu okha amene inu muli nawo, ndi, kubwera ku Kasupe wodzaza ndi Magazi otumphuka kuchokera mu Misempha ya Emanuele, pamene ochimwa agwera pansi pake, amataya banga lawo lonse la tchimo. Inde, bwana. Ndiwo maufulu okha amene inu muli nawo, ndi chifuniro-chawekha choperekedwa, kwa Mulungu, ndiyeno Mulungu amachita kutsogolera kuchokera pamenepo mpakana. Ndicho chimene chimapangitsa msonkhano... Ndicho chimene chimapangitsa zinthu zambiri zachirendo. Mzimu Woyera ukapita ku malo, Mzimu Woyera nkuti, “Izi si zolondola. Yimitsa msonkhano, sunthira kutsidya.” Ine ndiyimitsa iwo, aponso, m’bale, nkusunthira patsogolo. Ndiko kulondola, chifukwa iwe uyenera kutsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu. Ndipo njira yokha yoti utsogozeredwe ndi Mzimu wa Mulungu, ndi kukhalabe waulemu, osati kudziwa zambiri zonse.

<sup>98</sup> O, inu mukuganiza, “Ine ndikudziwa gawo lonse.” Eya, inu mwawutangwanitsa ubongo wanu wonse ndipo iwo sungakhoze ngakhale kugwira ntchito wokha. Inu mukudziwa mabuku onse ndi mayankho onse, ndi Chigriki chonse ndi Chihebri chonse, ndipo mulibe malo akuti Nkhunda iyikepo chisa. Ndiko kulondola. Koma inu mukudziwa izo zonse, ndiye Nkhunda siyingakhoze kutsogolera, chifukwa inu mukudziwa zochuluka kwambiri.

<sup>99</sup> Mwanawankhosa samadzinenera kuti amadziwa kanthu. Iye ayenera kukhala ndi winawake woti azimutsogolera iye. Ulemerero! Ndi zimenezo. Samadziwa kanthu! Ameni. Chinthu chokha chimene ine ndikuchidziwa, ndi, Khristu Yesu anafa kuti andipulumutse ine.

<sup>100</sup> Popita kupyola mu California uko kunali mnyamata akubwera, anali ndi cholembedwa patsogolo pa iye, anati, “Ine ndine chitsiru cha Khristu,” ndipo pa nsana anati, “Ndinu chitsiru cha yani?” Ndiko kulondola. Khalani chitsiru, kwa dziko, kuti inu mukhoze kutsogoleredwa ndi Mzimu Woyera, chifukwa ana aamuna ndi aakazi a Mulungu amatsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Aroma 8:1, anati, “Palibe kotero tsopano kutsutsika kwa iwo amene ali mwa Khristu Yesu, amene samayenda monga mwa thupi, koma Mzimu,” samayenda monga mwa nkhandwe, koma Nkhunda. Ameni.



<sup>101</sup> Doc anakonda kuyimba nyimbo, “Dzazitsani njira yanga tsiku lililonse ndi chikondi, pamene ine ndikuyenda ndi Nkhunda Yakumwamba; mudirole ine ndipite mwa kanthawi konse ndi nyimbo ndi kumwetulira, dzazitsani njira yanga tsiku lililonse ndi chikondi.” Lidzakhala tsiku la mtendere bwanji kwa Branham Tabernacle, kapena mpingo wina uliwonse kapena munthu aliyense, pamene iwo ati adzalanditse maufulu awo, kuti akhale mwanawankhosa.

“Funso lake ndi liti, M’bale Branham?”

<sup>102</sup> Bwererani kwa mwanawankhosa, bwererani kuti mukhale waulemu, bwererani ku kusadziwa kanthu, bwererani ku kungodzipereka nokha kwa Khristu. Musati muyesere, musati muyesere kuti mudziwe kanthu kena. Ingoyendani mofatsa, mwakachetechete, modzichepetsa, mwaulemu, ndipo Nkhunda idzakutsogolerani inu. Pakuti pamene inu muwona . . . kupita kukamvetsera miseche imeneyo, pamene inu mupita kukatenga kupsya mtima uko, pamene inu mupita mukuganiza kuti inu muli nawo ufulu wochitira *izi* ndi kuchita *izo*, Nkhunda imangotenga kuwuluka Kwake ndipo imapita basi kutali. Ndiye inu mulibenso Iyo. Tsopano, iyo siyiri kutali ndi inu mmawa uno, mpingo. Iyo yakhala kumene panja apo pa nthambi ya mtendere, kuyembekezera kuti chikhalidwe chanu chisinthidwe. Amen.

<sup>103</sup> Chimene inu mukusowa lero ndi kupereka maufulu anu onse, ndi kumulola Mulungu akugonekeni inu pansi ndi kusenga maufulu anu onse achoke pa inu. Amen. Kodi inu mukanakhoza kulingalira momwe mwanawankhosa wakale wamng’ono, ubweya wonse—wonse ukulendewera pa iye? Ndiwo maufulu ake. Eya. [M’bale Branham akufanizitsa mwanawankhosa wa wefuwefu—Mkonzi.] Ali kutenthedwa, ndiyeno nkungogona pa kama posengera. Iwo amadziwa chimene chiri choyenera kwa iye. Kutengera maufulu ake onse kutali kuwachotsa kwa iye ndi kuwusengapo iwo wonse, momwe iye amathamangira mozizirirapo ndi mopepuka. Mai, mai, iye ali wokondwa, ndipo amadumpha pozungulira ndipo amakhala ndi nthawi yayikulu. Inde, bwana. Ngati muti mulanditse maufulu anu, ndicho chimene inu muti mupeze. Koma inu muyenera kulanditsa maufulu anu ndi kulola Mawu a Mulungu asenge dziko lonse licho mwa inu, kutengera zizolowezi zonse za dziko kutali, ndipo inu mumakhala chorengedwa chatsopano mwa Khristu.

<sup>104</sup> Kuno nthawiyina kale, uko mu Afrika, ine ndinali kuyankhula kwa—kwa woyera wachikulire. Iye anati, “M’bale Branham, ine ndikudziwa kuti inu mumakhulupirira mu zauzimu.”

Ine ndinati, “Ndithudi, m’bale wanga.”

<sup>105</sup> Iye anati, “Zaka zapitazo ine ndinkakonda kuganiza kuti ine ndinali winawake.” Anati, “Ine ndinkaganiza ine ndinali Mkhristu weniweni.” Ndipo iye anati, “Ndiye kumtunda uko

mu mpingo wathu. . . Ine ndinkachita kukwera phiri, kumene ine ndinkayimitsa galimoto langa laling'ono." Ndipo anati, "Ine ndinkachita kukwera phiri pafupi, o, mitunda mazana atatu kapena anai, ndi kuzungulira matchire ndi zinthu, kuti ndikafike pamwambapo." Ndipo anati, "Ife tinkakhala ndi msonkhano wa pemphero pamwamba pamene." Ndipo anati, "Ine ndinkaganiza kuti ine ndinali Mkristu weniweni." Iye anati, "Ine ndinkalidziwa Baibulo lonse. Ine ndinaphunzira Chihebri chonse. Ine ndinaphunzira katchulidwe konse kolondola ka Mawu." Ndipo anati, "Aliyense ankayenda kudza kwa ine, ine ndimakhoza" [M'bale Branham akhwatichitsa chala chake—Mkonzi.] "kuyankhula kwa iwo monga choncho za Baibulo. Ine ndinkadziwa chimene ine ndinali kuchiyankhula." Iye anati, "Usiku wina ine ndinali kukwera kupita ku tchalitchi. Uko kunali kuli makangano ambiri mu mpingo wathu." Anati, "Uko kunali magulu pang'ono anali kutsutsana lina ndi limzake. Inu mukudziwa momwe iwo amawukirana."

Ine ndinati, "Inde, bwana."

<sup>106</sup> Iye anati, "Pa njira yanga pokwera phiri, ine ndinali kuyenda, ndipo zonse mwakamodzi ine ndinayamba kututumuka kuti winawake anali kunditsatira ine." Ndipo iye anati, "Ine ndinaganiza ine ndidikire pang'ono chabe kwa yense yemwe iye anali, kuti andipeze, ndipo kuti ine ndiyankhule nawo iwo kanthawi pang'ono pamene ife tinkapita tikukwera pa njirayi." Inu mukudziwa, ndiwo mtundu wa chinthu chabwino, iwe kungodikira kanthawi pang'ono. Ndipo akuti, "Pamene ine ndinayenda kukwera phirilo," anati, "Ine ndinabwera pamwamba. Mwamuna anabwera pamwamba pa phirilo," ndipo anati, "Iye anali ndi mtolo pa nsana Wake umene unali waukulu patali kumuposa Munthuyo." Ndipo anati, "Iye anali chabe wefufu ndi kumawuzira, ndi kumangopanga masitepe aafupi aang'ono, kuyesera kuti akwere pamwamba. Ndipo ine ndinati, 'Mnyamata, kodi ine ndingakuthandize Iwe kunyamula katundu uyu kukwera phirili?' Iye anati, 'Ayi, ine ndiyenera kumunyamula iye.'" Anati, "Ine ndinayang'ana pa dzanja Lake," anati, "Ine ndinadziwa ndiye kuti awo anali masomphenya. Iye anali ndi zipsyera mu manja Ake." Anati, "Ine ndinagwa pansu, ndipo ine ndinati, 'Ambuye, kodi Inu mukunyamula machimo a mdziko mu thumba limenelo?' Iye anati, 'Ayi, ine ndikunyamula ako okha. Kutu ndikufikitse iwe pamwamba pa phirili, kungoti kuti iwe ukhoze kukwera pamwamba.'"

<sup>107</sup> Ndimo momwe izo ziliri. Ngati ife titati tingoyang'ana pozungulira, ife tipeza kuti Iye akunyamula athu. Kodi izo sizimakupangani inu kudzimverera kuchepa? Mtima wathu wauthakati, wankhanza, basi chifukwa kuti ife tikhoza kuchita izo!

<sup>108</sup> Kuno nthawi yina kale ine ndinali kusaka. Monga inu mukudziwa, kuti ine ndimakonda kusaka. Ndipo uko kunali

mnyamata woyipa mu dziko limenelo, iye anali mnyamata woyipa. Ndipo iye anakakonda kumandiseka ine chifukwa ine sindimakhoza kuwombera mbawala ndi agwape aang'ono. Ine ndinati, "Ndi ubulutu." Ine ndinati, "Iwe bwanji osakhala msaki weniweni, waukhondo ndi kumawombera mbawala zokalamba ndi zinthu zimene ziri zokalamba ndi zokonzeka kuti zife? Mulungu anazipereka izo kwa ife. Kutilola tiamayi tating'ono ito ndi zinthu. . ."

<sup>109</sup> Iye anati, "Ha, ndiwe mlaliki, wa mtima-wankhuku!" Ankapitiliza kumandiiza ine monga choncho.

<sup>110</sup> Ine ndinati, "Tsopano, tapenya, ngati ine ndikanakhala wanjala ndipo ine ndimafuna imodzi ya agwape aang'ono awo, ine ndikukhulupirira Mulungu akadandilora ine ndikhale nayo iye. Koma kuiwombera chabe iyo kungoti ndichite mochenjera," chabwino, iye anakakhoza kudzazitsa ngolo phwamwamwa. Ndipo iye anapita ndipo anakadzipangira choyitanira, mtundu wina wa wenzulo, ndipo iye amakhoza kuwomba wenzulo imeneyo ndi kumveka chimodzimodzi basi ngati gwape wamng'ono akuyitana. Tsiku lina ife tinali mu thengo limodzi. Ine ndinamuchititsa iye manyazi, ine ndinati, "Ine ndikanadzichitira manyazi ndekha." Ankapha agwape asanu ndi atatu kapena khumi nthawi imodzi, ngati iye akanafuna, mbawala ndi chirichonse, basi kuti achite mochenjera, mwinamwake kudula miyendo yakumbuyo ndi kusiya zina zonse za iyo ziri pamenepo. Ine ndinati, "Iwe suyenera kutero."

"Ha," anati, "alaliki inu ndinu a mtima-wankhuku kwambiri!"

<sup>111</sup> Tsiku lina iye anayima mmbuyo mu tchire, iye anatenga nagwirizira wenzulo iyi ndipo iye anafuula, ndipo iyo inamveka ngati mwana wa gwape akulira. Basi pamene iye anachita izo, gwape wamng'ono wokongola anawonetsera mutu wake kunjira, kubwera akudumphira. Inu mukanakhoza kuwawona maso ake aakulu abulauni akuyang'ana. Iye anadabwitsidwa. Iye anali kuyang'ana pozungulira. Msakiyo anawerama, anasolola mfuti yake kuti awombere gwapeyo. Ndipo gwapeyo anamuwona msakiyo. Koma, inu mukudziwa chiyani, kufuula uko kwa gwape wamng'onoyo, iye sanali kuyiwona mfuti ija. Iye anali akufufuza kuli mwana ameneyo; amene anali mu vuto. Inu mukudziwa, kuwonetsera uko kwa umayi weniweni ndi chikondi cha mayi, kuti akhoza kuyang'anizana nayo mfuti ija pa maso, wa ku imfa, kuyang'ana pa iyo mu mpope wa mfuti imeneyo. Inu mukudziwa chiyani, kuwonetsera kumeneko kunali kwakukulu kwambiri, iye anayandikira pafupi kwa yekha, iye anaponyera pansu mfuti yake! Iye anathamangira mmbuyo ndipo anandigwira ine mozunguliza mkono, iye anati, "Billy, ndipempherere ine, ine ndakhala nazo zandikwana izi!"

Pamene iye anawona kuwonetsera uko kwa kulimba mtima kwa mayi!

<sup>112</sup> O, pamene dziko liwona kuwonetsera kwa chikondi cha Mulungu, ndi kulimba mu mtima wathu wa umunthu, ndi kusiyana kotani iko kuti kudzakhale. Pamene ife tilola Nkhunda ya Mulungu kubwera mu mtima wathu ndi kutipatsa ife ulemu, kutipanga ife ofatsa.

<sup>113</sup> Kumeneko mu tchire lamdima lija kuseri kumeneko, ine nditaima pamenepo ndikupempherera mnyamata wachikulire uja, ine ndinamutsogolera iye kwa Ambuye Yesu. Kuchokera pamenepo mpakana, iye anali wabwino, msaki waukhondo.

<sup>114</sup> Zedi, iye ankaganiza kuti iye anali nawo ufulu, iye akhoza kuchita chimene iye akanafuna kuchita. “Izo ziri pa malo anga, izo zimadya msipu wanga kumusi uko ngati izo zingafune kutero.”

<sup>115</sup> Ine ndinati, “Ndiko kulondola, koma si umunthu kuchita zimenezo.” Iwe uyenera kulantitsa maufulu ako. O Mulungu, chitani chifundo, kuti ife tizitero.

<sup>116</sup> Kuno nthawiyina kale, mu, o, pafupi zaka zana zapitazo, kunali Mkhristu wopambana amene anakhala kummwera chakumadzulo kwa United States. Dzina lake linali Daniel Curry, munthu wodabwitsa, munthu waumulungu, munthu woyera, Mkhristu weniweni, munthu amene aliyense ankaganizira zochuluka zake, munthu wodabwitsa chotero. Ndipo nkhaniyo imanena, kuti iye anafa kapena kuti anapita mu chizimbwizimbwi, ndipo iye anati. . . pamene iye anapita Kumwamba, ndithudi, pamene iye anafa. Ndipo pamene iye anakafika ku chipata changale, wosamalira anabwera ku chitseko, anati, “Ndiwe ndani?”

<sup>117</sup> Iye anati, “Ine ndine mlaliki, Daniel Curry, ine ndapindulira zikwi za miyoyo kwa Khristu. Ndipo ndine. . . ine ndikufuna kubwera mkati mmawa uno. Ulendo wanga wamoyo watsirizika pa dziko lapansi, ine ndiribe malo oti ndipiteko tsopano.”

<sup>118</sup> Ndimo momwe izo zikubwerera kwa inu mmawa wina, wochimwa. Ndimo momwe izo zikubwerera kwa inu, wobwerera mmbuyo. Ndimo momwe izo zikubwerera kwa inu amene mwakwiyitsa Mzimu Woyera nuchoka kwa iwo, osati nkumakhala aulemu ndi ofewa panonso. Inu mwakhala musanalire kwa zaka. Inu mwakhala musanachite manyazi, kwa ine sindikudziwa kuti ndi liti. Kudekha konse kwachoka kwa inu. Zedi. Koma iyo idzabwera pa khomo lanu umodzi wa mmawa uwu. Ndipo pamene Mzimu Woyera waulemu ubwera ndi kugogoda, bwanji inu osangoti mumulole Iye mkati?

<sup>119</sup> Kotero pamene Daniel Curry anafika uko ku—ku—ku chipata, iwo analowa mkati, anati, “Ife tiwone ngati inu muli nalo dzina lanu kuno.” Iwo anayang’ana ponse pozungulira, iwo

samakhoza kupeza dzina lirilonse. Anati, “Ayi, palibe Daniel Curry apa.”

<sup>120</sup> “O,” iye anati, “ndithudi!” Anati, “Ine ndine mlaliki.” Iye anati, “Ine ndapindulira miyoyo kwa Khristu.” Anati, “Ine ndayesera kuchita chinthu chimene chiri cholondola.”

<sup>121</sup> Wosamalira anati, “Bwana, ine ndine wachisoni kukuuzani inu, koma palibe Daniel Curry apa.” Anati, “Ine ndikuuzani inu chimene inu muti muyenere kuchita.” Anati, “Ife tiribe mafulu kuno kuti tiwutenge mulandu wanu.” Iye anati, “Koma kodi inu mukufuna kusumiranso mulandu wanu? Inu mukhoza kusumiranso iwo ku Chiweruzo cha ku Mpandowachifumu Woyera, ngati inu mukufuna kutero.” Koma anati, “Ife tiribe chifundo kuno kwa inu, nkomwe, chifukwa ife tiribe inu apa. Kulibe chifundo cha inu.” Anati, “Kodi inu mukufuna kusumanso mlandu wanu?”

Iye anati, “Bwana, ndi chiyandinso chimene ine ndingakhoze kuchita koma kusumanso mulandu wanga?”

<sup>122</sup> Iye anati, “Chabwino, ndiye, inu mukhoza kupita ku Chiweruzo cha ku Mpandowachifumu Woyera ndi kukasumiranso mulandu wanu kumeneko.”

<sup>123</sup> Daniel Curry ananena kuti iye anadzimverera yekha akupita kupyola mu kadanga kwa pafupi ora. Anati iye anafika mu malo, mmene munayamba kuwalira, kuwalira, kuwalira, kuwalira. Anati, pamene ankapita mopitirira, ndi pamene kunkakhala kowalira. Iko kunali kuchulukitsa mazana, nthawi za zikwi kowalira kuposa momwe dzuwa limawalira konse. Ndipo anati iye anali akunjenjera, kunjenjera. Ndipo anati, pamene iye anafika mkati mwake mwa Kuwala kumeneko, iye anamva Liwu likunena, “Kodi iwe unali wangwiro pa dziko lapansi?” Likungobwera kuchokera mu—mu Kuwala.

Iye anati, “Ayi, ine sindinali wangwiro,” anayamba kunjenjera.

Anati, “Kodi iwe nthawizonse unkasewera moona ndi aliyense?”

<sup>124</sup> Anati, “Ayi.” (Anati, “Zinthu pang’ono zinadza mu malingaliro anga zimene ine sindinali chimodzimidzi basi woona nazo.”) Anati, “Ayi, ine—ine—ine ndikulingalira ine sindinali woona.”

Anati, “Kodi iwe unkanena choonadi mu mulandu uliwonse, mu moyo wako?”

<sup>125</sup> Anati, “Ayi. Ine ndinakumbukira zinthu zina zimene ine ndinazinena, zimene zinalibe mthunzi...zimene zinali ndi mthunzi. Ine—ine—ine sindinali konse woona chimodzimidzi basi.”

126 Anati, “Ndiye, kodi iwe unayamba watengapo chirichonse chimene sichinali cha iwe, chirichonse, ndalama, china chirichonse chimene sichinali cha iwe?”

127 Anati iye ankaganiza pa dziko lapansi kuti iye anali wabwino ndithu, koma iye anatsutsika. Anati, “Ayi. Ayi, ine ndatengapo zinthu zimene sizinali za ine.”

Iye anati, “Ndiye iwetu sunali wangwiro.”

Iye anati, “Ayi, ine sindinali wangwiro.”

128 Anati iye ankayembekezera miniti iliyonse kuti kuphulika kuti kubwere kuchokera mu Kuwala kwakukulu kuja momwe Nkhunda inali, “Watsutsidwa!” Anati, basi ndiye iye anamva Liwu kuseri kwa iye, limene linali lokoma kuposa liwu la mayi lirilonse limene iye anayamba walimvapo. Anati iye anatembenuka kuti ayang’ane. Ndipo nkhope yokometsetsa imene iye anayamba wayiwonapo, yokoma kuposa nkhope ya mayi aliyense, inali itayima patsogolo pake. Ndipo anati Iye anati, “Atate, Daniel Curry anandiyimira Ine pansipo pa dziko lapansi. Izo nzoona, kuti iye sanali wangwiro, koma iye anandiyimira Ine. Iye anandiyimira Ine pa dziko lapansi, tsopano ine ndati ndimuyimire iye Kumwamba. Tengani tchimo lake lonse ndi kuwayika iwo pa kawundula Wanga.”

129 Ndi ndani yemwe ati akakuyimireni inu tsiku limenelo, m’bale, ngati inu mukumukwiyitsira Iye kutali nachoka kwa inu lero? Ine sindingakhoze kulalikirira mochulukiranso. Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

130 Wokonededwa Mulungu, wokonededwa Mwanawankhosa wakufa, wofatsa, wodzichepetsa, wonyozeka. Mbalame zinali nazo zisa ndipo nkhandwe zinali nazo mphanga, koma Inu munalibe malo, ndipo, komabe, Ambuye yemweyo wa Ulemerero! Pamene Inu munabadwa, iwo analibe zovala zirizonse zoti akuvekeni pa Inu. O Mulungu, zovala zanga zimandichitira ubwino wanji ine ndiye? Ndi ubwino wanji umene magalimoto amandichitira ine? Ndi ubwino wanji umene nyumba yabwino imandichitira ine? Ndi ubwino wanji umene ziti zidzachite tsiku limenelo? Inu munali opanda mzanu; panalibe aliyense anachita ubwanawe ndi Inu. Panalibe amene ankawoneka ngati wofuna kuti akupatseni Inu dzanja la chithandizo. Inu munanena kuti tsiku limenelo Inu mudzati, “Ine ndinali wanjala, inu simunandidyitse Ine. Ine ndinali wamaliseche, inu simunandiveke Ine.” Ndi ubwino wanji umene zonse zimene ife tiri nazo zoti tidzachite ife pa tsiku limenelo, Ambuye? Tiloreni ife tikuyimireni Inu, kotero kuti pamene ora ilo lifika, ndipo ife tiyenda kupita mu Kukhalapo Kwake, wamphamvuzonse, wopezekaponseponse, wodzi-... O Mulungu, pamene ife tikamva Nkhunda ija, ndi mapiko Ake itakhala kumbuyo uko mu Kuwala kwakukulu uko,

Iyo idzawalitsa kupyola mu Umuyaya wonse. Pamene, Inu mukukhala mu Kuwala!

<sup>131</sup> “Pamene ine ndidzayenera kuyima pamenepo mwa ndekha, m’bale wanga atapita, abusa anga atapita, amayi anga atapita, adadi anga atapita, mkazi wanga atapita, ana anga atapita. O Mulungu, kodi ine ndidzachita chiyani ndiye, Ambuye? Kodi ine ndidzachita chiyani ndiye? Ndipo izo zikhoza kukhala dzuwa lisanalowe usikuuno. Koma ine ndidzachita chiyani? Ine ndingakhoze kuchita chiyani? O Khristu, ine ndikuyimirani Inu tsopano! Ine nditenga kusankha kwanga lero. Ine ndilanditsa kuyankhula kwanga konse za anthu ena. Ine ndilanditsa kupsya mtima kwanga konse. Ine ndilanditsa kusiyana kwanga konse. Ine ndilanditsa chirichonse. Ndisengeni ine, Ambuye, tengani zonse zimene ine ndiri nazo. Inu mungonditenga ine, Ambuye. Ine—ine—ine ndikufuna kuyima mu malo Anu. Ine ndikufuna kusengedwa. Ine ndikufuna umbombo wonse, kunyada konse, kusayanjanitsika konse, basi zonse zitachotsedwa pa ine. Ndiye ine ndikufuna ndikuyimireni Inu, ngati mwanawankhosa wosengedwa, wololera kusiya zosangalatsa zonse za zomwe iwo amadzitcha zosangalatsa za moyo, kuvina konse, maphwando onse, zovala zonse zakale zoyipa, zopakapaka, utoto wa mmilomo, polishi ya mzikhadabo, kusayanjanitsika konse uku kumene kumawoneka ngati dziko. Inu munati, ‘Musati muchite konse ngati dziko. Musati muyanjane nalo konse dziko. Tulukani kuchokera pakati pawo!’ O Mulungu! Ndithandizeni ine, Ambuye. Ndisengeni ine lero. Nditengeni ine ngati mwanawankhosa ndipo mudirole ine ndikhale wosayankhula, ndisati nditseguke kamwa yanga, kusanena kanthu za izo, kungoyima ndikuti ndisengedwe.”

<sup>132</sup> O Mulungu, ndi kusiyana kotani izo zimapanga! Ine ndikukumbukira pamene Inu munandisenga ine kamodzi, munatenga mkazi wanga, mwana wanga, abambo anga, ndi m’bale wanga. Inu munandisenga ine mpala. Komabe, mu mtima mwanga, ine ndinkadziwa kuti ine ndinkakukondani Inu. Momwe Inu mwandidalitsira ine! Momwe Inu mwakhalira wabwino! Zonse zimene ine ndiri, zonse zimene ine ndikanakhoza kukhala, zonse zimene ine ndikanati ndidzakhale konse; ndi Inu, Mulungu, ndi Inuyo. Ine ndikuvomereza zolakwitsa zanga, ine ndikuvomereza zonse zimene ine ndinayamba ndachitapo kapena kulingalira. Ingondisengani ine, Ambuye, ine ndikufuna ndikhale mwanawankhosa Wanu.

<sup>133</sup> Osati zokhazo, Ambuye, koma mumutenge munthu aliyense mkati muno mmawa uno, nkghosa iliyonse, ndi iwo amene akanati afune kuti akhale nkghosa, asengeni onse a iwo, mmawa uno, Ambuye. Ikani phazi lawo laling’ono pozungulira zitsa za Uthenga. Mulole Mzimu Woyera uwatsogolere iwo ku kulapa tsopano lomwe, adziwe kuti akhala osayanjanitsika kwa Mulungu. Ndipo mulole Iye asenge kusayanjanitsika konse,

dziko lonse ndi zinthu zonse za mdziko. Inu muzisenge izo zonse zichoke mmawa uno, Ambuye, kuti ife tikhoze kuyima odekha ndi achete pamaso pa Inu, ngati Akhristu obadwa-kachiwiri. Perekani izo, Ambuye.

<sup>134</sup> Ine ndimakukondani Inu. Ine ndikufuna kupita, ziribe kanthu kaya nyengo ndi yotentha, kaya ine ndikumverera monga choncho kapena ayi. Ine ndikufuna kupita. Ine ndikufuna ndikuyimireni Inu, chifukwa ine ndikufuna Inu mudzandiyimire mulandu wanga tsiku limenelo, mudzati, “Chabwino, iye anandiyimira Ine, tsopano Ine ndimuyimira iye.” O Mulungu, perekani izo lero.

<sup>135</sup> Ndipo pamene mutu uliwonse waweramitsidwa, ndi mtima uliwonse utaweramitsidwa. Ine ndikudabwa mmawa uno ngati alipo chabe winawake pano amene akuzindikira kuti inu mwayesera kukhala nayo njira yanu yomwe, inu mwapanga zinthu izi zimene inu simumayenera kuzichita, ndipo inu mukungomverera mmawa uno kuti Ambuye angokusangani inu zichoke, ndi kunena, “Ndikupange iwe kukhala mwanawankhosa weniweni,” kodi inu mungakweze dzanja lanu. Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu, m’bale. Mulungu akudalitseni inu, m’bale. Winawake akuti, “Ndisengeni ine, Ambuye, ine ndayimirira. Ine ndine nkhusa. Ine sinditsegula nkomwe kamwa yanga, ine ndikungofuna Inu mudulire dziko lonse kutali litalikire kwa ine.” Mulungu akudalitseni inu, m’bale. Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu, mnyamata wamng’ono. Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu, mlongo. “Ndisengeni ine, Ambuye.” Mlongo Gertie. . . [Woyimba limba—Mkonzi.] Ndipo Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu, mlongo. “Ndisengeni ine tsopano, Ambuye. Ine—ine ndikufuna zinthu zonse za mdziko. . . Ine ndikufuna ndikuyimireni Inu mmawa uno. Ine ndikufuna kuyima ngati nkhusa yosengedwa. Ine ndikufuna zinthu zonse za dziko zidulidwe zitalikire kwa ine. Ine ndikufuna kuti ndikhale Wanu ndipo Inu mukhale wanga. Kodi Inu mundilandira ine, Ambuye, pamene ine ndikukwezera dzanja langa kwa Inu?” Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu, dona, ine ndikuwona lanu. Mulungu akudalitseni inu, m’bale wanga. Mulungu akudalitseni inu, dona wamng’ono. Ndizo zabwino. Mulungu akudalitseni inu kumbuyo uko, mayi. Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Ndiko kulondola, ingokhalani woonamtima. “Ine ndikufuna Mulungu kuti atenge zonse zitalikire kwa ine zomwe siziri zofanana kwa Iye, zolinga zirizonse zawumbombo zimene ine ndiri nazo, kusayanjanitsika kulikonse kumene ine ndiri nako.



Ine ndikufuna Iye andisenge ine njira yonseyo, mmawa uno. Ine ndikufuna kukhala monga Iye. Ine sindikusamala kaya pali mafulu kapena ayi; ine ndiribe ufulu ayi. Ine ndiri nawo kokha ufulu umodzi, ndipo ndiwo, kubwera kwa Ine. Iye amatenga zinazo.”

<sup>136</sup> Kodi alipo wochimwa pano amene sanavomerezepo Khristu kamodzi, sanapulumsidwepo konse, ndipo inu mukufuna kukumbukiridwa mu pemphero ili mmawa uno, kodi inu mungakweze dzanja lanu, mzanga wochimwa? Mulungu akudalitseni inu. Mmodzi wina kwezani dzanja lanu, mukuti, “Mundikumbukire ine, M’bale Branham. Ine si Mkhristu ayi, ndipo ine sindikudziwa basi nthawi imene ine nditi ndikakomane naye Mulungu. Ndipo ine—ine ndikufuna kukumbukiridwa pakali pano mu mawu a pemphero, pamene inu mukutseka.” Chabwino, kodi inu mungakweze dzanja lanu kuti ine ndikupempherereni inu? Iye akuwona. Mulungu akudalitseni inu, dona wamng’ono. Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mmodzi winawake, “Ine ndikufuna kuti ndikhale, ine ndikufuna . . .”

<sup>137</sup> Ndi angati muno amene ali obwererambuyo? “O,” inu mukuti, “Ine sindikanavomereza izo, M’bale Branham.” Koma, penyani, ngati Nkhunda ya chifatso iyo yachoka kwa inu, m’bale, apo pali chinachake chalakwika. Apo pali chinachake chalakwika pamene inu simungakhoze kupirirana wina ndi mzake. Pamene inu simungakhoze kukhululukira munthu aliyense kuchokera mu kuya kumene kwa mtima wanu, ziribe kanthu zimene iwo achita kapena zimene iwo anena, ngati inu simungakhoze kuwakhululukira iwo kuchokera mu kuya, Yesu anati, “Ngati inu simukhululukira munthu aliyense zolakwitsa zake, kuchokera mu mtima mwanu, ngakhalenso Atate anu Akumwamba sakukhululukirani inu.”

<sup>138</sup> Tsopano, bwanji ngati, nyengo yotentha iyi, bwanji ngati lero Mulungu atakuyitanani inu? Pamene pali Kasupe wotseguka, mpingo wokonzeka, Mzimu Woyera wakhala pano pa mathero kumene a nyumba iyi, wokonzeka kubwera pansu kumene ndi kubwerera mu mtima mwanu ndi kukupangani inu aulemu ndi a mtendere. “Ndiyenera kuchita chiyani ine, M’bale Branham?” Ingokhalani mwanawankhosa. Mzimu Woyera ubwera pansu kumene pamene inu mukhala mwanawankhosa. Koma ngati inu muli ndi zolinga zolakwika, lolakwika—lingaliro lolakwika, mukufuna kukhala ndi njira yanu yanu, ndipo nkusalolera kulanditsa iyo, ndiye Mzimu Woyera sudzabwera konse.

<sup>139</sup> Tsopano ndi mitu yathu itaweramitsidwa, ine ndikudabwa ngati aliyense wa inu amene mwakweza dzanja lanu . . . Tsopano, Yesu anati, “Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha, sadzabwera konse mu chiweruzo koma wadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo,” Yohane Woyera 5:24. Koma

tsopano ngati inu mukanafuna kubwera ku guwa, gwadani pansi apa, tiyeni tipemphere limodzi mpaka kumverera kwaulemu, kwa mtendere uko kumene inu munakhalapo nako, kapena mukanafuna mutakhala nako, kutabwera pa inu kachiwiri. Pamene ife tirikusunga mitu yathu yoweramitsidwa, pamene ife tirikuyimba, “Pali Kasupe wodzazidwa ndi Magazi,” ine ndikufuna inu mubwere, dzagwadani pansi ndi kupemphera. Aliyense tsopano amene akufuna kubwera, dzagwadani pansi apa pa kanjira ka pa guwa ndi kupemphera kanthawi.

Kuli Kasupe wodzazidwa ndi Magazi,  
Wotumphikira kuchokera mu Mtsempha wa  
Emanuele,  
Ndipo ochimwa akagwetsedwera mkati...  
(Mulungu akudalitseni inu, dona,  
dzibweranibe ndi kudzagwada pansi)  
Ataya . . .

<sup>140</sup> Ndi mitu yanu yoweramitsidwa, monga ine ndikuyembekeza kuti inu mwachita mu mtima mwanu. Inu mukudziwa yemwe wayamba kubwera mu kampata mmawa uno, ziyenera kukupangani inu kuchita manyazi ndi inueni? Mkazi wachikuda, chinthu chosawuka, wa mopindira manja motupa, tsitsi lotuwa, akupanga njira yake kupita ku guwa.

<sup>141</sup> Kuno nthawiyina kale, bambo wachikulire wachikuda anapulumutsidwa, mu nthawi ya ukapolo. Iye anapita, ndipo pamene iye anapulumutsidwa, iye anamuwuzwa bwana wake kuti iye anali mfulu. Iye anati, “Ndiwe chiyani?”

Anati, “Ine ndine mfulu.” Ndiye iye anamupanga iye mfulu.

<sup>142</sup> Pano pakubwera gulu lina la anthu likubwera kuno kufuna chipulumutso mmawa uno. (Anati iye anali mfulu.) Aliyense mu pemphero, ndipo muzipemphera zolimba ngati inu mungatero, pamene Mzimu Woyera ukuchita ndi anthu kupanga malingaliro.

Iye anati, “Mose, kodi iwe ukuti unali mfulu?”

Anati, “Inde, bwana, wamkulu. Ine ndine mfulu.”

<sup>143</sup> Anati, “Ngati uli mfulu, ndiye ine ndati ndikupange iwe kukhala mfulu, inenso. Pita uzikalalikira Uthenga.”

<sup>144</sup> Pamene iye anakonzekera kuti afe, ambiri a abale ake oyera anabwera mkati kuti adzamuwone iye, ndipo pamene iwo anatero, iye anati, ankaganiza kuti iye anali mu kukomoka. Pamene iye anawukapo, iye anati, “Ine ndimagaliza kuti ine ndinali nditapita.” (Mulungu akudalitseni inu, m’bale wanga, gwadani kumene pansipo.) Anati, “Ine ndimagaliza ine ndinali nditapita kale.”

Anati, “Kodi iwe unawona chiyani, Mose?”

<sup>145</sup> Iye anati, “Pamene ine ndinayenda kulowa mu chipata, ine ndinawona Iye.” Anati, “Ine ndinali nditayima,

ndikuyang'ana pa Iye." Ndipo ndinati, "Apo panali Mngelo amene anabwera ndipo anati, 'Dzibwera kuno, Mose. Iwe walalikira Uthenga zaka zambiri, iwe uli ndi mwinjiro ndi korona zimene zikukuyembekezera iwe.'" Iye anati, " 'Musati muyankhule kwa ine za mwinjiro ndi korona. Ine sindikufuna mwinjiro ndi korona ayi. Ine ndikungofuna kumayang'ana pa Iye.'" Ine ndikuganiza ndicho cholinga cha Mkhristu aliyense.

<sup>146</sup> Kuno nthawiyina kale, kutali kuchokera ku Chicago, ine ndinali mu coliseum, kosungira zakale, kani, ndipo ine ndinali kuyang'ana monse mozungulira mmenemo. Ine ndinamuwona Mniguro wachikulire, nkhatu yaying'ono yoyera ya tsitsi kuzungulira mutu wake, akusuntha mozungulira pamenepo, ali ndi chipewa mu dzanja lake. Ine ndinayang'ana pa iye. Iye anayang'ana mu malo aang'ono, ndipo iye analumphira mmbuyo, ndipo misozi inayamba kutsikira pansu pa tsaya lake lokalamba lakudalo. Iye anayamba kupemphera. Ine ndinamupenyererera iye kwa kanthawi pang'ono. Iye anapenyanso kachiwiri, anayamba kulira kachiwiri. Ine ndinayenda kupitapo ndipo ine ndinati, "Bwana."

Iye anati, "Inde, mzanga woyera?"

Ine ndinati, "Ine ndikukukuwonani inu muli... Nchiyani chakutengani inu chotero? Inu mwatengeka chotero ndi chiyani?"

<sup>147</sup> Iye anati, "Bwana, ngati inu mungakhoze kumverera m'mbali mwanga, ine ndiri ndi zikang'a pozungulira mu mbali yangayi." Anati, "Ine nthawiyina ndinali kapolo." Iye anati, "Mu mphanga yaying'ono ya gilasi iyi apa, ndi chovala chiri mmenemocho."

Ine ndinati, "Ine ndawona chovala, koma ndi chiyani chachirendo cha icho?"

<sup>148</sup> Iye anati, "Banga ilo apo," anati, "amenewo ndi magazi a Abraham Lincoln." Anati, "Magazi amenewo anavula lamba la ukapolo kulichotsa pa ine." Iye anati, "Tsopano, bambo woyera, kodi izo sizikanakhala ngati zokutenga iwe, nawenso?"

<sup>149</sup> Ine ndinayika mikono yanga mozungulira khosi lake lokalamba, ine ndinati, "Mulungu akudalitseni inu, m'bale. Ine ndikudziwa Magazi ena amene amanditenga mtima ine."

Iye anati, "Ine ndikuwadziwa Magazi amenewo, inenso, bambo."

<sup>150</sup> Ine ndinati, "Iye anachotsa lamba la ukapolo kulichotsa pa ine." Nthawi ina ine ndinkatuluka Lamlungu ndi kukathamanga ndi kumapitiriza, ndi kumanena nthabwala zoyipa. Ndipo, O Mulungu, ine ndinkachita chotani izo? Mukanali zipsyera umo mu mtima mwanga momwe ine ndinkachitira izo. Koma ine ndiri woyamikira kuti Iye anavula lamba kulichotsa pa ine. Izo zonse zapita tsopano, Iye anayima mu malo anga.

<sup>151</sup> Kuno nthawiyina kale, ndikuyang'ana pa mkazi, ndipo iye anali woyipa kwambiri ine ndinkafuna kumuweruza iye. Mulungu anandipatsa ine masomphenya. Ine ndinamupempherera iye pamenepo, pakuti ine ndinawona kuti machimo anga anali chimodzimidzi aakulu monga akewo. Ndipo ine ndinayenda kupitapo ndi kukakhala pansu pambali yake ndi kumuchititsa iye manyazi, ndinamuza iye kuti ine ndinali mtumiki. Abwenzi ake aamuna awiri. . . Iye anali pafupi makumi asanu ndi limodzi mphambu zisanu kapena makumi asanu ndi awiri, abwenzi ake aamuna awiri anagwada pansu pomwepo, ndipo iwo onse anapereka mtima wawo kwa Khristu. O, mai, ndi kusiyana kotani!

<sup>152</sup> Kodi simutero inu? Kodi inu mwachimwa basi mochuluka choncho, mmawa uno, kodi mwawupanga basi mtima wanu mwakuda chotero ndi wamwaye mpaka ngakhale Mzimu Woyera sungakhoze konse kuwukhudza iwo? Mwinamwake Nkhunda yatenga kuwuluka Kwake Kwamuyaya, Iwo wapita kwa nthawizonse.

<sup>153</sup> Mulungu akudalitseni inu, wokonedwa. Msungwana wamng'ono akuyenda. Mulungu akudalitseni inu, wokomamtima. Inu mukuti, "Msungwana wamng'ono uyo sakudziwa." O, inde, iye akudziwa. Iye sanawerenge basi magazini ochuluka ndi nkhani zochuluka za chikondi monga inu nonse mwachitira. Ndilo vuto, iye ndi wanthete. Yesu anati, "Lolani ana aang'ono adze kwa Ine."

<sup>154</sup> Winawakenso angafune kuti abwere, kudzalumikizana nawo pozungulira mmawa uno? Guwa ndi lotseguka. Mphindi ina chabe, ndiye pamene ife tikuyimba kamodzinso, ndiye ife tipereka pemphero pamene ochimwa olapa awa ali kupemphera.

Wakuba pakufa anasangalala kuwona  
Kasupe uyo mkati. . . (Zedi, chirichonse  
chinali chitapita, munthu wosawukayo anali  
athedwa.)

Ndipo apo mulole ine, ngakhale woyipa monga  
iye. . .

<sup>155</sup> Kodi inu simubwera kuno tsopano? Kodi inu simubwera kuno, inu amene mukudziwa bwino? Baibulo linati, "Ngati iwe udziwa kuchita bwino, ndipo nkusachita icho ayi, kwa iwe ndi zoposa tchimo." Kodi inu simubwera? Inu mukudziwa kuti inu mwalakwitsa. Pangani njira yanu ndi kudzagwadwa pozungulira guwa, ndi kumuwuza Mulungu kuti muli wachisoni chifukwa cha momwe mumachitira naye Iye. Mulole Mzimu Woyera ubwerere ndi kudzakupangani inu wofatsa ndi waulemu ndi wodekha kachiwiri. Kodi inu simutero? Kumbukirani, ngati inu mufa, ndipo Iye nkukhala kuti atakuchokerani inu, palibe aliyense woti akakupepetsereni mulandu wanu. Iye akufuna

inu mumuyimire Iye mmawa uno. Mulungu akudalitseni inu, m'bale wanga.

<sup>156</sup> Kuyembekezera. Kodi ndi okhawa, khumi ndi asanu basi mu mpingo amene mukumverera kwenikweni kuti mwatsutsidwa? Inu mwakhala moyo wa mtendere, wofatsa, waulemu, wodekha? Tsopano, izi zikulondoleredwa ndi Mzimu Woyera. Kodi ndinu wokhululukira, mulibe adani? Mukukhala moyo mopyola, apamwamba pa kutsutsika kwa, ochimwa? Inu simumakhala monga achikunja, inu mukukhala moyo mosiyana? Moyo wanu wonse ndi wokonzedwa mosiyana? Mzimu Woyera waulemu ukukhala pa mpandowachifumu wa mtima wanu, kukupangani inu kukhala moyo wa mtendere ndi wodekha ndi wokonda, pozungulira anthu onse? Oyandikana nawo anu ndipo onse amadziwa, ndipo oyanjana nawo anu onse amadziwa, kuti ndinu waulemu, wodekha, wofatsa, Mkristu wodzichepetsa? Nkhunda ya Mulungu ili ndi inu? Inu mukutsimikiza? Uwu mwina ukhoza kukhala mwayi wanu wotsiriza. Chabwino.

<sup>157</sup> Ndiye kwa inu pano pa guwa, Mulungu akudalitseni inu. Inu simusowa kuti muweruzidwe tsopano. Mzimu Woyera wabweretsa chiweruzo kwa inu. Ndipo inu simunayesere kuti mugwire maufulu anu, kunena, "O, ine ndakhala Mkristu nthawi yayitali mokwanira. Ine sindikusowa kuti ndipite." Ena a inu, nthawi yanu yoyamba kudzakhala konse pa guwa. "Ine ndikhoza kukhala wochimwa ngati ine ndikufuna kuteru, ndiwo ufulu wanga." Eya, ndiko kulondola. Inu ndinu wochita mwaufulu wanu, inu mukhoza kuchita mwa njira iliyonse imene inu mukufuna. Koma inu mwalanditsa maufulu anu mmawa uno. Kunena kuti, "Kodi iwo anena chiyani, ine wodzinenera Chikristu ndiyeno nkupita pa guwa, kodi iwo anena chiyani?" Koma Mulungu akuti chiyani? Iye anati kuti inu mubwere, ndipo inu munachita izo. Tsopano inu munalanditsa maufulu anu, inu muyenera kubwera pokhala nawo Mzimu Woyera waulemu kuti utenge malo Ake mu mtima mwanu lero. Ine ndikudziwa kuti Iye achita izo. Ine ndikudziwa kuti Iye atero. Iye analonjeza kuti Iye adzatero. Apo, Iwo sungakhoze basi kuthandizira izo, sungakhoze basi kudziletsa kubwera. Iye akupempha, akulira, anafa, ndi china chirichonse, chifukwa cha malo oti abwereko, kufuna kuti abwere kwa inu.

<sup>158</sup> Ndipo mu malo anu a imfa, pamene mngelo wa imfa akukhala pa phazi la kama wanu, mmalo moyang'ana kunja uko pa chinthu chowopsya, ndi kumadziwa kuti inu munakana kuti mubwere nthawi yina, ndiyeno moyo wanu unakhala wakuda ndi wamwaye, palibe nthawi inanso, ziribe kanthu kaya inu mutalira molimba chotani. Esau anachimwa tchimo lake la chisomo. . . tsiku lake la chisomo, kani, ndipo sanapeze mwayi. Iye analira molimba, kuyesera kuti apeze malo woti akakonzere izo, koma iye samakhoza kuchita izo. Mulungu anamuyitana iye nthawi yotsiriza.

159 Koma inu mukulanditsa maufulu anu onse ndi abwenzi anu onse, ndi kumverera kwanu konse ndi chirichonse, mmawa uno, kuti mubwere pano. Inu mwalanditsa maufulu anu, kudzagwada pansi apa ndi kuyankhula kwa Mulungu. Ine ndikukuuzani inu mwa Mawu a Mulungu, kuti Khristu anati, “Iye amene abwera kwa Ine, ine sindidzamataya kunja mwanjira iliyonse.” Tsopano pamene inu muli apo pa guwa, lapani, muuzeni Iye kuti inu mukupepesa kuti inu munachita zimene inu munachita.

160 Ndilo vuto limene anthu samalandirira Mzimu Woyera pamene iwo abatizidwa, iwo samalapa bwinobwino. Mulungu akuyesera kuwapatsa iwo Mzimu Woyera. Iye akufuna inu kuti mukhale ofatsa ndi aulemu, achete. Ndicho chifukwa inu mumapitiriza ndi kudzikonda komweko mu mtima mwanu. O, inu mukhoza kuwukapo, kufuula, kuyankhula mu malirime, kapena aliyense, izo sizingakupangeni inu kukhala nawo Mzimu Woyera. Inu muyenera kuwuka kuchokera pamenepo munthu wosiyana. Inu muyenera kuwuka kuchokera pamenepo, waulemu, wodekha ndi wofatsa, wodzichepetsa, ndipo Mzimu wa Mulungu ukukhala mwa inu. Chaka chotsatira, kuyang’ana mmbuyo mmusi mu kanjira ndi kuwona kutali kumene inu mwafika, kuwona kuti inu mukutha mtunda nthawi zonse. Ndiwo Mzimu Woyera. Mzimu Woyera ndi chikondi, chimwemwe, mtendere, kupirira, kufatsa, ulemu, kupirira, chikhulupiriro. Tsopano, ingolapani ndi kumuuzza Mulungu kuti inu mukufuna izo pakali pano, Iye ndi . . . Iye adzachita izo.

161 Msungwana wamng’ono, iwe kumeneko, wokonedwa, iwe uchite chinthu chomwecho. Akudalitse iwe. Mayi ako ayima ndi manja awo ali pa iwe.

162 Mlongo wokonedwa wachikuda wachikulire apa, atawerama pa guwa. Inu mwina mumachita kudya zigumu za chimanga ndi phala la mgayiwa, mwina mumachita kumakhala mu kangalande, chifukwa cha zonse zimene ine ndikuzidziwa, mlongo. Mulungu adalitse mtima wanu, ilipo nyumba yachifumu yokonedwera inu mu Ulemerero mmawa uno. Kulondola.

163 Penyani pansi pa guwa ndipo muwone dona, akuyamba imvi, mkazi wamng’ono amene mutu wake uli pansi, mkazi wa tsitsi-loyera-kwenikweni. O Mulungu! Muwoneni mwamuna atagwada, osiyana awo motsatira apa. Zingolapani, muwuzeni Iye kuti inu mukupepesa. Muwuzeni Iye kuti inu simudzazichita izo kenanso. Mwa chisomo Chake, inu mungolola zosiyana zanu zipite, kuchokera lero mpakana. Inu mukufuna kukhala waulemu ndi wachete. Inu mukufuna kukhala wodzichepetsa ndi kupita kumene Iye akukutsogolerani inu.

164 Pamene anthu anena chinachake, ziribe kanthu momwe izo ziziwoneka zolondola chotani, inu mukalanditsa maufulu anu kuti muyankhule za woyandikana naye wanu. Inu mukayankhula, inu mupita muzikayankhula za Yesu. Inu

muzikachita kokha chinthu chimene chiri cholondola. Inu simukati muzipita kunja ngati wakupha. Inu simuti muzikapita kunja kuti mukalumphere pa osalakwa. Koma inu mukuwona sewero lamphamvu lija la kulimbamtima kwa Akhristu enieni, ndipo inu mukufuna kuti mukhale monga iwo. Inu simudzasowa kuti mumuwuze aliyense kuti ndinu Mkristu, ngati inu muli mmodzi, iwo amangowona izo ndi kudziwa izo pamene inu muyankhula. Inu mwasindikizidwa mkati ndi kunja.

<sup>165</sup> Tsopano, pamene inu mukuchepetsa mtima wanu, lapani tsopano. Muwuzeni Mulungu kuti ndinu “wachisoni,” inu “simuchita izo kenanso,” inu “mukuchita manyazi” ndi inueni, momwe inu mukuchitira. Ndiyeno ine ndati ndikupempherereni inu. Ndipo ine ndikukhulupirira, pomwepo, mtendere ungokhazikika pa mtima wanu, mtendere basi ngati mtsinje ubwera ukusefukira mmusi mu moyo wanu. Inu mwina simuchita kukhala mukufuula, inu mwina simuchita kukhala mukuyankhula ndi malirime, inu simuchita mwina kukhala mukudumpha mmwamba ndi pansu; koma inu mudzakhala mukuchoka pa guwa ndi Chinachake mwa inu, Chinachake mwa inu chimene chiti chidzakumangirireni inu ku mtanda wakale wopumphunthika utali wonse womwe inu muli moyo. Tsopano pempherani, pamene ine ndikutero. Lapani.

<sup>166</sup> Atate athu Akumwamba. Zolengedwa zosayenera, chipinda chotentha ichi, cha thukuta mmawa uno, bokosi la thukuta; koma, Mulungu, Inu munachitira thukuta ilo kutulutsira ife. Mizimu Woyera bwerani pansu, anthu okhutitsidwa kuti iwo anali olakwa. Iwo anali akuchimwa. Mizimu yawo inali yamwano. Iwo anakhala awukali, amsunamo, odziwa-izo-zonse, osafuna kulolera kuti alape, osafuna kulolera kuti awakhululukire anthu amene achita zinthu zowatsutsa iwo. Iwo sanali lolera kutero, koma lero Mizimu Woyera watenga Mawu a Mulungu, kuwayika Iwo mu mitima yawo yaulemu yomwe, ndi kunena, “Tsopano kodi inu mukufuna kubwerera kumene inu munali nthawi yoyamba yomwe inu munabwera ku guwa, kubwerera kumene aliyense, inu muzikakonda aliyense, ndipo inu mundikonde Ine ndi chikondi chosafa? Ndiye ingowukanipo ndi kubwera kuno ku guwa.” Iwo achita izo, Ambuye.

<sup>167</sup> Tsopano, ine ndikupemphera tsopano kuti Inu muyeretse malingaliro awo, Ambuye, yeretsani mitima yawo, kuwapanga iwo aulemu ndi amtendere. Mulole iwo akawuke kuchokera pa guwa ili tsopano, iwo atatha kulapa, kupereka miyoyo yawo mpaka kwa Inu, kubwerera mmbuyo ku makwawo. Ziribe kanthu chimene chiti chikhale chikuchitika, ngati mwamuna akhala yense wokwiya, kapena mkazi akhala yense wokwiya, kapena woyandikana naye ali wokwiya, kapena winawake amene inu mukugwira naye ntchito kapena kuyanjana naye, “Ine ndizingokhala waulemu ngati nkunda.”

168 Zikatha zonse, kubwezera Kwanu ndi kwa Inu, “Ine ndidzabwezera, atero Ambuye.” Momwe ife tapezera izo kukhala chomwecho, Ambuye. Ingoyimani njii, khalani aulemu, muwone Mulungu akutenga. . . akubwera kumene kwa mwanawankhosa Wake. Ndithu, ndithudi. M’busa wabwino uyu anapereka Moyo Wake chifukwa cha iwo, Iye anabwera kumene kwa nkhosa Zake. Ndipo Iye azitsogolera izo. Tsoka kwa ameneyo yemwe awakwiyitsa iwo pamenepo! Tsoka kwa ameneyo yemwe anena liwu limodzi mowatsutsa iwo! Anatero, “Kukanakhala bwino kuti mwalawamphero ukanamangidwa pa khosi lako, ndi kumizidwa mu kuya kwa nyanja. Angelo awo nthawizonse amawona nkhope ya Atate Anga amene ali Kumwamba.” Mwaona? O Mulungu, ife tikufuna. . . “Ndipo pamene inu mukuchita kwa iwo, inu mukuchita kwa Ine.”

169 Kotero, Mulungu, ine ndikufuna kukhala waulemu. Ine ndikudziyika inemwini pa guwa, inenso, mmawa uno; osati mmawa uno, koma mmawa uliwonse ndi tsiku lililonse. Ine ndikufuna kukhala wodekha ndi waulemu, ndi monga Yesu. Perekani izo, Atate. Tithandizeni ife kuti tikhale chotero tsopano, mulole mafunde akuya a chikondi atembenezikire pa moyo wathu.

Mtendere! Mtendere! Mtendere wodabwitsa,  
Kubwera pansu kuchokera kwa Atate  
kumwamba; (Kodi inu simukuwumverera  
Iwo tsopano mu mtima mwathu?)  
. . . pa mzimu wanga kwa nthawizonse,  
(Aleluya! Aleluya!) . . .

170 Mlongo Gertie anati uwuzeni mpingo wonse iye watsutsidwa, nayenso, koma iye akupanga limba guwa lake. Pakuti guwa, limba ndi guwa lake, anati, “Muwuwuze mpingo undipempherere ine,” pamene iye wakhala pamenepo ndipo misozi ikuyenderera pansu kuchokera pansu pa mandala ake. Gome ili ndi guwa langa. Ine ndalapa, inenso, Baibulo langa lanyowa. O Mulungu!

Mtendere, mtendere wa Mulungu!  
Kubwera pansu kuchokera kwa Atate  
kumwamba; (O, aleluya!)  
. . . pa mzimu wanga kwa nthawizonse.

171 Mulungu, ngati ine ndachimwira motsutsa aliyense, motsutsa Inu, tengerani izo kutali, Ambuye. Tengerani tchimo kutali uchoke ku mpingo wanga wawung’onowu mmawa uno.

172 Ndi angati amene angakhoze kumverera basi kuti Mulungu wakukhulukirani inu, ndipo Nkhunda ya Mtendere ikukhala pa mtima wanu kachiwiri? Iyo yawuluka mobwerera posakhalitsa kumene, yatenga apo malo Ake. Mzimu Woyera wangosunthira mmbuyo ndi kunena, “Mwana Wanga, Ine ndakhala ndikufuna kuti ndizikonda iwe nthawi zonse. Iwe



sumandilora basi Ine kuti ndizichita izo. Ine sindingakhoze kukhala ndi mzimu wako wakale wodzikonda. Koma tsopano pakuti iwe wagonjera izo, Ine ndabwereranso ku mtima wako mmawa uno.” Ndi angati amene akumverera mwa njira imeneyo? Kwezani dzanja lanu. Kwezani dzanja lanu, ndiko kulondola, ponseponse pa guwa. O, ndizo zabwino. Ndi angati kunja mwa omvera amene akumverera mwa njira imeneyo? Kwezani dzanja lanu. O! [M’bale Branham anena kwa walimba, “Kukhala Monga Yesu.”—Mkonzi.]

<sup>173</sup> Atate athu Akumwamba, ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha nthawi iyi ya kudzipereka kofewa, ngati kutenga apulo mu dzanja, kulifinya ilo, kulisupula ilo, mpaka ilo litafewa, kufewa chotero mwakuti mwana wamng’ono akhoza kukhala pansu ndi kumalidya ilo. Ndimo momwe ife tikufunira mitima yathu, Ambuye. Itengereni iyo mu dzanja Lanu la-zipsyera, ingoyisendani iyo, kunena, “Mwana, kodi iwe sukuwona kuti iwe wandipweteka Ine? Iwe unali kundipweteka Ine pamene iwe unawuluka molekerera pa chigwiriro monga choncho. Iwe unali kundipweteka Ine, o, Mtima wanga unangowukhira kwa iwe, mwana, pamene Ine ndinakuwona iwe ukuchita zinthu *zakuti-ndi-zakuti*. Koma tsopano pakuti Ine ndatengera mtima wako mu dzanja Langa, Ine ndikufuna kuwupanga iwo wofatsa kwenikweni. Ine ndikufuna kuwupanga iwo kotero kuti Ine ndikhoza kuwugwiritsa iwo ntchito ndi kukhala mwa iwo. Ine ndikufuna kuwuluka mobwerera pa chisa mmawa uno, Ine ndikufuna kuwuluka mobwera ndi kudzakhalamo, kupanga mokhalamo Mwanga ndi iwe.” Perekani izo, Mulungu. Ife timakukondani Inu. Perekani izo, kwa ulemerero Wanu. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu.

Kukhala monga Yesu, ku... (Kodi inu simukukonda kupembedza basi monga chonchi? O, moyo wanga ukungosamba.)

Pa dziko lapansi ine... (Kumuwona Iye akubwera pansu mwa—opembedza monga chonchi, mtima wanu ukumverera mwaulemu kwenikweni? Mtima wanga ukungogunda mothamanga.)

...ulendo kuchokera pa dziko kupita ku Ulemerero

Ine ndingopempha kukhala monga Iye.

Kodi inu mungakweze dzanja lanu pamene ife tikuyimba iyo?

Kukhala monga Yesu, ku... .

(Joe, iwe ukufuna kubwera kuno ndi kudzapemphera mmawa uno, m’bale? Mulungu akudalitseni. Pezani inu malo pano

pa guwa, M'bale Joe. Mulungu akudalitseni inu.)

...ulendo kuchokera pa dziko kupita ku Ulemerero

Ine ndikungopempha kukhala monga Iye.

<sup>174</sup> Ine ndikudziwa kuti kuli kotentha, abwenzi. Ine ndikudziwa kuti iko kuli. Koma ine—ine ndikuyembekeza inu mukumverera basi monga ine ndikuchitira. O, ine ndikungomverera ngati ine ndikanangowulukira kutali. Momwe Iye aliri wokonda! Ine ndingakhoze kuchita chiyani? Ine ndikanapita kuti? O Mulungu! Kodi ine ndikupita kuti? Kodi ine ndalunjika wa kuti? Kodi icho chikakhala—chikakhala chiyani? Ine ndikakhala kuti zaka zana kuchokera pano? Bwanji ngati ine ndikanakhala ndiribe Iye? Nkuti, nkuti kobisala kulikonse kwina?

Kuchokera ku khola la ku Betelehemu kunachokera Mlendo,

Pa dziko ine ndifuna kukhala monga Iye;

Monse kupyola ulendo wa moyo kuchokera pa dziko kupita ku Ulemerero

Ine ndikungofunsa kukhala monga Iye.

Tonse palimodzi tsopano.

Kukhala monga Yesu... (Matamando akhale kwa Mulungu! Inde, Ambuye! Inde, Ambuye! Osati dziko; monga Inu!)

...kukhala monga Iye;

Monse kupyola ulendo wa moyo kuchokera pa dziko kupita ku Ulemerero

Ine ndikungopempha...

<sup>175</sup> Inu mukanali chiweramitsire mitu yanu, ine ndati ndikufunseni inu chinachake. Winawake muno akukwiyitsa Mzimu Woyera. Winawake wayitanidwa. Ine ndikuyankhula mu Dzina la Ambuye Yesu, ngati mneneri Wake. Ine ndikukhoza kumverera mtima Wake utavulazidwa. Kunja uko, winawake sanamumvere Iye, akanayenera kubwera. Kodi inu simubwera tsopano?

Monse kupyola ulendo wa moyo kuchokera...

(Inde, mlongo, koma alipo oposa inu)... Ulemerero

Ulemerero

Ine ndikungopempha kukhala monga Iye.

Kungokhala monga Yesu... (Ndicho chonse chokhumba changa, wofatsa ndi wotsika, wodzichepetsa, kukhala monga Iye.)

Pa dziko lapansi ine... (Kodi inu simubwera kuno tsopano? Mulungu akufuna akuwoneni inu mukupanga kusuntha, mulipo angapo a inu.)

Monse kupyola...

176 Ine ndimadziwa kuti inu munali kubwera, Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Ndi zimenezo. Ndi zimenezo. Ine ndinayang'ana kunjira pa omvera awa, ndipo mthunzi wowopsyesetsa wakuda utapachikika pamenepo umene ine sindinawuwonepo konse. Mzimu Woyera uli pano tsopano. Iwo uli kumanja kwanga tsopano. “Kuwukwiyitsa Mzimu Woyera.”

Kukhala monga Yesu . . .

177 Kodi Iye anachita chiyani? Ankapita kumene Atate ankamutsogolera. Mulungu akudalitseni inu, m'bale. Mulungu akudalitseni inu, m'bale wanga. Ndiko kulondola, dzisunthiranibe kuno ndi kugwada pansa.

Pa dziko lapansi ine ndikuyembekezera . . .

178 Tsopano ndiyo nthawi ya kulapa kwa nthawi-yakale, kuwongola, kupanga mokonza. Dzibwerani kuno. Ndikumvererabe kuti alipo ochuluka mmenemo. Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Ndiko kulondola. Mzimu Woyera nthawizonse ndi wolondola. Bwerani tiyeni. Ndiko kulondola, sunthirani patsogolo choncho.

Iye, kukhala monga Yesu, kukhala monga, inde, Yesu,

Pa dziko lapansi ine . . . (O, mai, ndiko kulondola! Ndiyo njira yake, ingodzazitsani timipata, sunthiranibe patsogolo choncho ndipo pempherani.)

Kupyola ulendo wa moyo kuchokera ku dziko kupita ku Ulemerero, (Ingolapani, muwuzeni Mulungu kuti ndinu opepesa, ndicho chonse chimene inu muyenera kuchita.)

. . . kukhala monga Iye.

179 Kodi inu simuti muzibwerabe tsopano? “Kwa . . .” Ndiko kulondola, ingophwasulani momasuka ndithu, dzibwerani. “Kukhala monga . . .”

180 Kodi inu mukanachita chiyani? Ndi ndani yemwe ati akakuyimireni inu, mwinamwake usikuuno? Ndi ndani yemwe ati akakuyimireni inu pamene imfa ibwera pa mkono wamalaya wanu? Ziribe kanthu zomwe inu mwachita, Mzimu Woyera wakhala pomwepo apo pafupi ndi inu. Ndi Iyeyo amene akufuna kuti inu mubwere.

Monse kupyola ulendo wa moyo kuchokera pa dziko kupita ku Ulemerero.

181 Ingolapani, nenani, “Mulungu, ine ndikupepesa. Ine—ine sindikanafuna kuti ndichite zimenezo. Inu simudzandiyimira ine ngati ine sindikuyimirani Inu tsopano. Ndipo ine ndikufuna Inu

mudzandiyimire ine, ndipo ine ndikukuyimirani Inu kuchokera lero mpakana. Ine ndikakhala monga Mkhristu ayenera kutero. Ine ndisintha njira zanga. Ine ndikakhala waulemu ndi wodekha. Ine ndikalola aliyense achite kuyankhula kwawo komwe, chirichonse. Ine ndikangokhala wofatsa ndi wodekha pamaso Panu.” Ziribe kanthu kaya ndi motalika bwanji inu mwadzitcha kuti muli Mkhristu, mpingo umene inu muli wake, izo ziribe kanthu kochita ndi izo. Bwerani tiyeni. Mulungu akudalitseni inu. Sunthirabe kunja, mwana.

<sup>182</sup> Mulungu akuyankhula ndi iwe tsopano. Ngati inu mukundikhulupirira ine kuti ndiri wantchito Wake, Mzimu Woyera unayankhula kwa ine mmawa uno, unati, “Kapange kuyitana kumeneko, alipo ochuluka kumeneko.” Tsiku lake ndi lino, nthawi yake ndi iyi. Alipo pafupi asanu kapena asanu ndi mmodzi kumbuyo uko, kwenikweni iwo ayenera kubwera tsopano. Kumbukirani, m’bale, mlongo, ine ndikuyang’ana kumene pa inu, ine ndikuwona mithunzi yamdima iyo itapachikika pa inu. Ndi bwino mubwere kuno pakali pano.

<sup>183</sup> Kukhala monga Yesu! Kodi inu simukufuna kuti mukhale monga Iye, aulemu, odekha, ofatsa, odzichepetsa? Mulungu akudalitse iwe, mnyamata wamng’ono. Mulungu akudalitseni inu, bambo amene muli ndi mwana. Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Mulungu akudalitse iwe, mzanga wochimwa. Ndiko kulondola. Sunthirani patsogolo, mlongo, zibwerani choncho, ingodzipezerani nokha malo. Mulungu akudalitseni inu.

<sup>184</sup> Mlongo wokonedwa, inu muli nazo zambiri zoti muthokozere. Mutagona pa kama, mukufa, pano inu mukuyenda kupita, guwa. Mulungu adalitse mtima wanu wanthete.

<sup>185</sup> Mzimu Woyera ukuyankhula kachiwiri tsopano. Kulapa, ingolirilani apa kwa Mulungu, zingopempherani pemphero lanu lomwe. Ndinuyo amene mwachita kuchimwako, tsopano ndinuyo amene muti muchite kupempherako. Muwuzeni Mulungu kuti ndinu wo pepesa chifukwa cha chimene inu mwachita. Musati mupereke chidwi chirichonse kwa yemwe ali pozungulira inu. Ingonenani, “Mulungu, mundikhulukire ine, ine sindimatanthauza kuti ndikhale monga choncho. Ine ndikufuna kukhala waulemu. Ine sindidza—ine sindidzayipidwa konse ndi kumakangana kenanso.”

<sup>186</sup> O Mulungu, o, momwe ine ndikukondera izo! Atate Akumwamba, chifukwa cha aliyense wolapa amene pansu pa guwapo tsopano, kuwera pa bondo lawo, akupemphera! O Mulungu, mulole amayi, adadi, ana, atate, amayi, ena alionse, oyandikana nawo, mamembala a mpingo, madikoni, matrastii, O Mulungu, pa nthawi-yowumbanso iyi ya kachitidwe-kachikale, amene akhala mu chipinda chotentha ichi mmawa uno, Mzimu Woyera ukubwera kumene pansu, ukuyankhula mtendere. O Mulungu, ine ndikufuna kudzayima tsiku limenelo

kuti ndidzakumveni Inu mukunena, mwaulemu, “Inde, iwe unabwera ndi kudzandiyimira Ine, tsopano Ine ndikuyimira iwe.” Ine ndikufuna Inu muyike mtendere umenewo mu mtima uliwonse umene uli pano lero, Mulungu. Mwakachetechete ndi mwaulemu, ine ndikufuna Inu kuti muchite izo. Ine ndikufuna Inu kuti mungosunthira mkati mmenemo ndi kumverera koteroko komwe kuti kusadzawasiyenso iwo kenanso, kuyambira lero mpakana mtsogolo. Mulole makomo akakhale atsopano. Mulole anthu akakhale anthu atsopano. Mulole chirichonse chikakhale chatsopano lero, chifukwa anthu awa adzichepetsa okha. Inu munati, “Ngati anthu amene atchedwa ndi Dzina Langa ati adzadzichepetse okha, ndi kupemphera, ndiye Ine ndidzamva kuchokera Kumwamba.” Ndipo ine ndikudziwa kuti Inu mukutero, mmawa uno, Mulungu.

<sup>187</sup> Ndipo ine ndikupempherera chikhululukiwo kwa iwo amene anatsalira mokhala mwawo, amene akanayenera kubwera. Mulungu, yankhulani kwa iwo, ndipo mulole iwo asakakhale nawo konse mtendere pa dziko lapansi mpaka iwo atapanaga lingaliro limenelo, Ambuye, kuti abwere ndi kuti adzapangidwe bwino ndi Inu. Perekani izo, Ambuye. Mudalitse wina aliyense tsopano. Mulole kukoma Kwanu ndi chifundo Chanu zizikhala nthawizonse pa moyo uliwonse umene ukudzimvera chisoni ndi kubwera mu mpingo uno mmawa uno.

<sup>188</sup> Atate, Mulungu, ine ndachita izi mwa kuyitana Kwanu. Ine ndawayitana anthu awa; iwo ayima. Inu munati, “Iye amene ati adzandichitire Ine umboni pamaso pa anthu, iyeyo Ine ndidzamchitira umboni pamaso pa Atate anga ndi Angelo oyer.” Ambiri a awa pano akhala Akhristu kwa zaka, koma iwo ayima mmawa uno kuti achitire umboni machimo awo kuti iwo achita zolakwika. Iwo akhala osakondeka. Mzimu Woyera unali utapita kuchoka kwa iwo. Ndipo nthawi zambiri zimene iwo sangakhoze kumverera kumverera kwaulemu, kokoma, kofatsa uko kumene iwo amayenera kumakumverera. Ambiri a iwo ndi ochimwa amene abwera kwa nthawi yawo yoyamba. Koma, Atate, iwo akufuna kumverera kodabwitsa uko, mtendere umene umapyola kumvetsa konse. Kuperekeni iko kwa iwo tsiku ili, Ambuye Mulungu, ndipo mulole iwo palimodzi akhale okondeka ndi odzaza ndi Mzimu Woyera, pamene iwo akuchoka malo ano lero, kuti azipita ku nyumba zawo zosiyana, ndi kukhala moyo wosiyana ndi kuti akakhale anthu osiyana. Ife tikupempha izi mu Dzina la Khristu.

<sup>189</sup> “Malo Pa Kasupe.” Chabwino, inu amene muli paguwa, imirirani, yang’anani mmwamba kwa Ambuye Mulungu, tembenukani gwiranani chanza ndi aliyense pozungulira inu. O, ife tati tiyimbe nyimbo, aliyense tsopano, pamene ife tiri kuyimirira mphindi yokha usanayambe msonkhano wamachiritso.


Malo, malo, inde, alipo malo,  
Alipo malo pa Kasupe a inu;  
Malo, malo, inde, alipo malo,  
Alipo malo pa Kasupe a inu. (Aliyense!)

Malo, malo, inde, alipo malo,  
Alipo malo pa Kasupe a inu;  
Malo, malo, inde, alipo malo,  
Alipo malo pa Kasupe a inu.

Malo, malo, inde, alipo malo!  
[Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

<sup>190</sup> Chikhulupiriro! Inu mukudziwa tsiku lina, m'bale, pamene anu—akazi anu anayitana, kuti apemphereredwe chifukwa cha inu? Tinapita mu chipinda momwemo, ndipo Mzimu Woyera unanena kwa ine, “Usati uwope.” Ameni. Kodi Iye sali weniweni? Zodabwitsa! Chabwino, yamikani Ambuye! Ine ndikungomverera ngati ndifuule chigonjetso! Chabwino.

Ndipo Magazi Ake atsuka moyera . . .” (Muli  
ndi chinachake choti munene?)  
Yesu amapulumsa!

<sup>191</sup> Chabwino, M'bale Neville tsopano. Ndipo M'bale Slaughter ali ndi mawu woti anene. [M'bale Slaughter ayankhula. Malo osajambula pa tepi—Mkonzi.] Ambuye alemekezeke! [M'bale Neville anena, “Ine ndikukhulupirira aliyense waulandira mmawa uno.”] Ulemerero! Aleluya! Aleluya! [M'bale Neville ayankhula, ndiyeno iye akuti, “Mukumbukire misonkhano usikuuno, ife tiri ndi kutsukana-mapazi ndi utumiki wa mgonero.” Iye akumupempha M'bale Branham, “Kaya inu mukhalapo kuno?”] Ine mwinamwake ndidzakhala kuno usikuuno, inenso. Inde, monga momwe ine ndikudziwira, ine ndidzakhala kuno kupatula ine nditayitanidwa kwinakwake. 

*Mpingo Ndi Chikhalidwe Chake*  
(*The Church And Its Condition*)  
Ogasiti 5, 1956, Lamlungu Mmawa

*Khwalala Ndiro Chipata*  
(*Strait Is The Gate*)  
Marichi 1, 1959, Lamlungu Mmawa

*Mpingo Wonyengedwa Ndi Dziko*  
(*A Deceived Church, By The World*)  
Juni 28, 1959, Lamlungu Mmawa

Mauthenga awa a M'bale William Marrion Branham, anaperekedwa pachiyambi mu Chingerezi ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., atengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito ndipo anasindikizidwa mu Chingelezi. Maulaliki awa anamasuliridwa mu Chichewa ndi kudindidwa mu 1997 ndi:

CHICHEWA

©1997 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)